# *Yehova-Yire* [1]

Khalani pansi. Uwu ndi mwayi waukulu, kuti ndabwereranso usikuuno. Ndipo dalitso lalikulu kwa ine, kubwera ndi kudzayankhula kwa inu za Ambuye wathu Yesu, Yemwe ine ndikutsimikiza kuti ambiri a inu mukumudziwa, kapena ine ndikuyembekeza inu mutero, mu kukhululukidwa kwa machimo anu ndi—ndi mwa njira ya chisomo Chake, kwa inu. Ndipo mulole Iye agawire kwa inu, usikuuno, zochuluka za chisomo Chake. Pamene ife tizichoka pano, ife tidzakhoze kunena, monga iwo akubwera kuchokera ku Emau, "Mitima yathu inatentha mkati mwathu, pamene Iye anali kuyankhula nafe mkati mwa njira."

2 Tsopano, mmawa uliwonse, ine ndikukhulupirira iwo ali naye a—a—a—munthu wapagulu ngati iye. Bambo Vayle pano ali ndi a—phunziro, kukhala ngati kuyankha mafunso ndi kuyankhula pa Lemba. Kodi izo ndi muno mchipinda chino? Mchipinda momwe muno, mmawa. Ndipo ngati aliyense ali womasuka, ndipo atumiki ena, kapena ena otero, atafuna kuti adzacheze, bwanji, aliyense ndi wolandiridwa. Ndipo M'bale Vayle ndi mphunzitsi wakuya ndithu. Kwenikweni, iye ali ndi maphunziro abwino.

3 Ndipo chotero, ine ndinanena tsiku lina, ine—ine ndikanakonda ndikanakhala ndi maphunziro. Ine ndimayenera kugwiritsa ntchito mafanizo, monga chinachake chimzake, kuti ndifotokoze, inu mukudziwa. Ine ndiribe maphunziro okwanira kuti ndizilongosole izo. Koma mwanjira ina, kapena imzake, Ambuye amandithandiza ine kuti ndizipereke izo.

4 Ndipo chotero ine ndikukumbukira, nthawi ina panali a—munthu mu Lemba, dzina lake linali Yohane, ndipo abambo ake anali wansembe. Kawirikawiri, iwo ankatsatira zimene bambo awo ankachita. Koma iye analidi ndi uthenga; iye anali woti adzalengeza Mesiya. Ndipo tsopano ngati iye anapita ku sukulu kumene bambo ake anapita, iwo anati, "Tsopano, inu mukumudziwa M'bale Wokondedwa *Wakuti-ndi-wakuti*? Ameneyo ndi Mesiya basi," iwo pafupifupi anamupangitsa iye kuti ayankhule zimenezo. Kotero, onani, iye sanapite ku sukulu iliyonse ya mtundu umenewo.

5 Iye anapita ku chipululu, kumene iye anakaphunzira za Mulungu. Inu mukuzindikira mauthenga ake, akututuluka? Iye analibe nkomwe maphunziro. Iye analowamo ali ndi zaka naini, anatuluka pa sarte, analalikira miyezi sikisi, ndipo anaphedwa. Tsopano ife tikupeza kuti iye anagwiritsa ntchito . . . Anati, monga Afarisi anatulukira, ndi Asaduki, ndipo iye anati, "Oh, inu m'badwo wa njoka!" Ndicho chimene iye anachiwona

mu chipululu; njoka, chinachake chimene chiri chonyansa ndi chowonda, ndi chonyenga. Mukuona?

6 Tsopano winawake akanakhoza kunena kuti, "Bwanji, iwe kachidutswa kakang'ono kopandapake," kapena chinachake. Koma iye . . .

7 Koma, onani, iye sankadziwa mawu oti agwiritse ntchito, kotero iye ankangoti, "Inu m'badwo wa njoka," ndicho chimene iye anachiwona mu chipululu. Anati, "Ndani wakuchenjezani inu kuti muthawe mkwiyo ulinkudza? Musati muyambe kunena, kuti 'Ife tiri, ife ndi a *izi* ndipo ndife a *izo*,' chifukwa Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi," zomwe iye anaziwona, "kuti awukitse ana kwa Abrahamu. Ndipo nkhwangwa yaikidwa pa muzu wa mtengo." Iye ankadziwa zoyenera kuchita ndi mtengo woipa. "Uliwonse umene sukubala zipatso zabwino, udzadulidwa pansi ndi kuponyedwa pamoto," kuwotcha nkhuni zoipazo.

8 Mwaona, uthenga wake wonse unali chinachake cha chirengedwe, iye amachifanizitsa icho. Anthu wamba amamvetsa zimenezo. Ndiyeno iwo . . . Ine ndikuganiza nthawizina zikhoza kukhala zabwinoko pang'ono kutero kuposa mawu onse akulu opambana awa omwe anthu amaphunzira ku sukulu.

9 Tsopano, ife tinali mochedwa pang'ono usiku wathawu, kotero ife tikuyesetsa kukutulutsani inu pa nthawi yake, usikuuno, ngati ife tingakhoze kutero. Ndipo ine ndikudalira kuti Ambuye salola kuti mvula igwe moyipa kwambiri usikuuno, pa denga la malata ili, kotero ife tingokhulupirira ndi—ndi kuyesera kumutumikira Iye, mwakudziwa kwathu kopambana.

10 Tsopano tiyeni tiyime pamene ife tikuwerenga Mawu a Mulungu, pamene ife tikuwerenga tsopano kuchokera mu Bukhu la Genesis. Ndipo ife tikuyambira pa mutu wa 22 ndi ndime ya 7, kuwerenga ya 14, kuphatikiza.

> *Ndipo Isaki ananena kwa Abrahamu atate wake, ndipo anati, atate Anga: ndipo iye anati, Ndine pano, mwana wanga. Ndipo iye anati, Taonani moto ndi nkhuni: koma mwanawankhosa wa nsembe yopsyereza ali kuti?*
>
> *Ndipo Abrahamu anati, Mwana wanga, Mulungu adzazipezera yekha mwanawankhosa wa nsembe yopsyereza: chotero iwo anapita onse a iwo pamodzi.*
>
> *Ndipo iwo anafika kumalo komwe Mulungu anamuuza iye; ndipo Abrahamu anamanga guwa kumeneko, ndipo anaika nkhunizo mwa dongosolo, ndipo anammanga . . . mwana wake* yemwe, *ndipo anamugoneka iye pa guwa pa nkhuni.*
>
> *Ndipo Abrahamu anatambasula dzanja lake, ndipo anatenga mpeni kuti amuphe mwana wake.*

*Ndipo mngelo wa* A*MBUYE* *anamuyitana iye kuchokera kumwamba, ndipo anati, Abrahamu, Abrahamu: ndipo iye anati, Ndine pano.*

*Ndipo iye anati, Usaike dzanja* lako *pa mwanayo, ngakhale kuti iwe* uyike...pa *iye: pakuti tsopano Ine ndikudziwa kuti ukuwopa Mulungu, poona* wakaniza...*sunandikanize* wako...*mwana yekhayo wochokera kwa ine.*

*Ndipo Abrahamu anakwezera maso ake mmwamba, ndipo anayang'ana, ndipo taonani kumbuyo kwake mwanawankhosa wamphongo anagwidwa mu nkhalango ndi nyanga: ndipo Abrahamu anapita ndipo anakatenga mwanawankhosa, ndipo anakampereka iye kwa nsembe yopsyereza mu...mmalo mwa mwana wake.*

*Ndipo Abrahamu anatcha dzina la malowo Yehova-yire: monga kwanenedwa mpaka lero, Mu phiri la* A*MBUYE* izo zidza*woneka.*

11 Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha ndi kupereka pemphero.

12 Atate athu a Kumwamba, ife tikuwuzidwa ndi Mawu awa, amene ali Mulungu, kuti, "Chikhulupiriro chimadza pakumva, ndipo pakumva kwa Mawu a Mulungu." Ndipo tsopano, Atate, ife tikupemphera kuti Inu mupereke kwa ife nkhani ya kuwerenga uku, kuti ife tikhoze kuphunzira monga zimauzidwa kwa ife ndi Baibulo, kuti, "Zinthu zonsezo mmbuyo mu Chipangano Chakale zinali zitsanzo zomwe ife tiyenera kuziwona." Kwa iwo amene amamvera kuitana kwa Mulungu, ndi odala. Iwo amene amakana, ndi otemberereredwa. Kotero ife tikupemphera, Atate, kuti ife tikhale nako kumvetsa, usikuuno, mwa vumbulutso. Mulole Mzimu Woyera uwululire kwa ife zinthu zomwe ziri zokhudza ife mu tsiku lino, zonsezo ndi zobisika mu chinsinsi chachikulu ichi cha Mulungu chimene chakhala chiri chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

Inu mukhoza kukhala pansi.

13 Ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa phunziro, Ambuye akalola, kuchokera ku lingaliro la: *Yehova-Yire*. Mawuwa amatanthauza "Mulungu adzadzipezera Yekha nsembe."

14 Ndipo ife tikuyankhula za Abrahamu, ndipo iyi inali nthawi imene iye anali kuyembekezera mwana wolonjezedwa. Kuti tipeze choonadi chenicheni cha izi, ife tibwerera. Ndipo izi zinali mu mutu wa 22. Ife tikufuna tikachezerenso mmbuyo; ine ndiri ndi Malemba angapo ndawalemba apa, amene ine ndikufuna kuti ndizilozerako, ngati nkotheka. Ndipo ndikufuna kuti ndiyankhule pa zimenezo, ndipo ndikufuna kuti ndiyambire pa mutu wa 12. Ife tibwerenso kuti tikapeze kuti Abrahamu

uyu anali munthu wotani, ndipo tsopano bwanji—zinatheka bwanji kuti Mulungu amusankhe iye.

15 Ife tikudziwa kuti lonjezo linaperekedwa kwa Abrahamu ndi Mbewu yake ya pambuyo pake, ndipo kungokhala mwa Abrahamu ife tiri olowa limodzi ndi Iye ndi lonjezo. Tsopano Abrahamu anali ndi mbewu, ndipo mbewuyo, ndithudi, inali, iye anali ndi mbewu zambiri, zimbewu, koma iye anali ndi Mbewu imodzi imene inali ya lonjezo. Iye anali ndi Ishmaeli; ndiyeno Sarah atafa, iye anakwatira mkazi wina ndipo anabala ana amuna seveni pambali pa ana aakazi; ndipo onsewo ndi mbewu ya Abrahamu, koma a . . . zimbewu za Abrahamu, koma Mbewu inali imodzi yomwe inali nalo lonjezo. Ndipo Mbewu, kwenikweni, ndi *chikhulupiriro* cha Abrahamu, chimene iye anali nacho mu Mawu olonjezedwa a Mulungu.

16 Tsopano Abrahamu, ife tikupeza kuti, ife . . . sakuwonekera mpaka ife titamupeza iye pano pafupifupi mutu wa 12. Mutu wa 11 wa Genesis, ife tikupeza kuti abambo ake anabwera kuchokera ku Babulo. Ndipo Abrahamu anali munthu wamba chabe, chimodzimodzi monga inu kapena ine, kapena wina aliyenseyo. Ndipo iye anali akukhala, kani, zomwe ife tingaziganizire, munthu wokalamba. Iye anali zaka sevente-faivi zakubadwa. Iye anali atamukwatira mlongo wake wa theka. Dzina lake anali Sarah. Ndipo dzina lake nthawi imeneyo, ndithudi, silinali Abrahamu, ilo linali Abramu. Ndipo—ndipo mkaziyo linali Sarai. Kotero ife tikupeza kuti iye anali wamng'ono kwa zaka teni kwa iye, zomwe zinamupangitsa iye sikisite-faivi, ndipo iye zaka sevente-faivi zakubadwa.

17 Iwo mwinamwake, iye anali mlimi, ankakhala mu chigwa cha Shinara kumeneko, ndipo ankakhala moyo wamba. Iye—iye mwinamwake ankapita kumeneko masana, ndipo amakatenga nyama yake kuthengo, ndi kuthyolako nthudza, ndipo ankakhala moyo wa mtundu umenewo. Munthu wamba basi, panalibe chirichonse chapadera chokhudza iye. Koma tsiku lina, Mulungu anamuyitana iye. Ndicho chimene chinapangitsa kusiyana, pamene Mulungu anapanga kuitana.

18 Ndipo umo ndi momwe ziliri ku moyo uliwonse. Izo zimatengera Mulungu. Si zomwe iwe umachita; ndi zimene Mulungu amachita. Mukuona? Inu mumati, "Ine ndinamufunafuna Mulungu. Ine ndinamufunafuna Mulungu." Inu mukulakwitsa. Palibe munthu amamufunafuna Mulungu. Mulungu amamufunafuna munthu. Mukuona? Si inu kumufunafuna Mulungu; ndi Mulungu kukufunani inuyo.

19 Yesu anati, "Inu simunandisankhe Ine, koma Ine ndinakusankhani inu." Mukuona? Kotero inu munasankhidwa asanaikidwe maziko a dziko lapansi, kapena inu simunasankhidwe nkomwe. Iye anangobwera kuti adzawombole dzina limenelo. Ndipo onse amene maina awo siali pa Bukhu la

Moyo wa Mwanawankhosa limenelo. . .asanaikidwe maziko a dziko lapansi, ndi okhawo ati adzakhale kumeneko, mulimonse. Mwaona? Inu munasankhidwa mwa Iye asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Pamene Mwanawankhosa anasankhidwa, ndiye inu munasankhidwa ndi Iye, asanayikidwe maziko.

20 Ndipo inu ndinu, monga ine ndinanenera usiku wathawu, chikhumbo cha kuganiza kwa Mulungu. Mwaona, ndiyo njira yokhayo yomwe inu mungakhoze kukhalira Wamuyaya, ndi mawonekedwe okhawo a Moyo Wamuyaya. Alipo mawonekedwe amodzi okha a Moyo Wamuyaya, ndipo ndiwo Mulungu. Kotero, ndizo zonse, Iye ndi Mmodzi yemwe ali Wamuyaya.

21 Tsopano ife tikupeza kuti Abrahamu anali nawo malo amenewo. Ndipo Mulungu, mu Chipangano Chakale, ankachita ndi zoimira ndi mithunzi, kuti akasonyeze chimene Iye akanati adzachite.

22 Tsopano ife tikupeza apa kuti Mulungu anayankhula kwa iye. Ndipo chinthu chachikulu, Mulungu atamuyitana iye. . .Kuitana kumene Mulungu anapereka kunali kuyitana kwauzimu. Koma, komabe, izo sizinakhoze kumudzandimitsa konse Abrahamu, panalibe nthawi. Iye nthawizonse ankadziwa kuti ameneyo anali Mulungu. Ndicho chinthu chopambana. Pamene. . .

23 Maitanidwe a Mulungu ndi auzimu; palibe chirichonse chachibadwa. Mulungu amatenga chauzimu ndi kuchichita icho mwachibadwa, koma maitanidwe a Mulungu ndi auzimu. Baibulo linati, "Mphatso ndi maitanidwe sizimasowa kulapa." Mwaona, izo zinadzodzedweratu ndi—ndi Mulungu.

24 Tsopano ife tikupeza kuti, mu izi, kuti Abrahamu pokhala anaitanidwa, iye anamva liwu la Mulungu, ndipo Iye anamuuza iye chinachake chimene chinali pafupifupi chosatheka. Iye pokhala wa zaka sevente-faivi zakubadwa, mkazi wake wa zaka sikisite-faivi zakubadwa, izo zikanamupanga iye pafupifupi zaka twente kupitirira kusintha kwa thupi, ndipo anakhala ndi iye kuyambira ali mtsikana. Iwo analibe ana. Ndipo, komabe, anamuuza iye kuti adzakhala ndi mwana, ndipo kudzera mwa mwana uyu dziko lonse, mafuko onse, akanadzadalitsidwa. Tsopano icho ndi chinthu chachirendo.

25 "Ndipo Abrahamu," Baibulo linati mu Aroma mutu wa 4, "sanazandime pa lonjezo la Mulungu mu kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu."

26 Ine ndikhoza kulingalira, pambuyo pa mwezi woyamba. . . Ndithudi, Sarah, monga ine ndinanena, anali atadutsa kusintha kwa thupi. Mwezi woyamba, ine ndikhoza kulingalira Abrahamu anati, "Sarah, ukumverera bwanji, wokondedwa?"

"Palibe kusintha."

27 “Chabwino, adalitsidwe Mulungu kuti ife tikhala ndi mwanayo, mulimonse. Ife tikhala naye iye basi. Mulungu anati ife tinali.”

28 Sarah, analuka nsapato zazing’ono, ndipo anatenga matewera ndi mapini, ndi chirichonse; anakonzekera, kumukonzekera iye, chifukwa iye ankadziwa kuti iye adzakhala naye iye. Mulungu ananena chomwecho. Mukuona?

29 Chaka choyamba chinadutsa. “Iwe ukumverera kusintha, wokondedwa?”

“Palibe kusintha nkomwe.”

30 “Mulungu alemekezeke! Icho chidzakhala chozizwitsa chachikulu tsopano kuposa momwe icho chinaliri nthawi yoyamba. Mwaona, padutsa chaka. Tikhala naye iye, mulimonse.” Chifukwa chiyani? Mulungu ananena chomwecho. Izo zikukhazikitsa izo. Mulungu ananena chomwecho. Ife... Mulungu ananena chomwecho.

31 Zaka teni zinadutsa. “Kodi ukumverera bwanji tsopano, wokondedwa?” Pano iye ali sevente-faivi, ndipo iye ali eyite-faivi.

32 Tsopano kodi inu mungalingalire mwamuna wachikulire ndi mkazi monga choncho, lero, akupita ku chipatala, ndi kukati, “Dokotala, ife tikufuna tipange madongosolo. Ife tidza...”?

33 Mulungu amakufunsani inu kuti mukhulupirire zina mwa zinthu zopusa, koma Iye nthawizonse amazipanga izo kukhala bwino. Mulungu...Munthu amene amakhulupirira Mulungu, mwamtheradi amachita mwa misala, kwa dziko lapansi.

34 Kodi inu mungalingalire Mose, wophunzitsidwa mu zonse—nzeru za Aigupto, mkulu wa asirikali, a—a—a—ankhondo a Igupto. Ndipo, komabe, zaka forte izo zinamutengera iye kuti aphunzire mpaka zimenezo, ndipo izo zinamutengera Mulungu zaka forte kuti achotse maphunziro amenewo mwa iye, basi zomwe zimatengera dziko kuti liyike mwa iye. Zaka forte zowonjezera, Iye anamuphunzitsa iye zonse, maphunziro onse, fioloje kuchoka mwa iye. Ndipo Iye anakomana naye iye kuseri kwa chipululu, ndipo iye anadziwa zochuluka za Mulungu, mu maminiti faivi mu Kukhalapo kwa Mulungu, kuposa momwe iye anaphunzirira zaka forte kuchokera mmabuku. Ndiko kulondola.

35 Mulungu samadziwika ndi maphunziro. Iye amadziwika ndi chikhulupiriro. Ndipo Mulungu anayankhula ndi iye mu zauzimu. Ndipo ndi chinthu chopusa bwanji, nthawizina, Mulungu amatipangitsa ife kuchichita.

36 Kodi inu mungalingalire bambo wachikulire, usinkhu wa zaka eyite, akuthamanga, mneneri akumuthawa Mulungu? Ndipo mu Kukhalapo kwa Mulungu maminiti faivi: mmawa wotsatira (kodi inu mungamuganizire iye?), bambo wokalamba,

ndevu zikulendewera pansi monga *chonchi*; mutu wake wadazi ukunyezimira; ndodo yokhota mdzanja lake; mkazi wake atakhala pachishalo cha bulu, ndi mwana m'chuuno mwake; panjira akupita!

"Iwe ukupita kuti, Mose?"

"Ndikupita uko ku Igupto, kuti ndikalande."

37 Onani, "kukalanda," kuwukira kwa munthu mmodzi. Izo zikumveka zopusa. Koma, chinthu chake chinali, iye anachita izo, chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Izo zikukhazikitsa izo.

38 Pamene Mulungu anena chomwecho, ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo. Ndizo—ndi zimenezo. Ngati Mulungu anapanga lonjezo, pachikani moyo wanu pa ilo. Ngati inu mungakhoze kukhulupirira ilo, pachikani wanu. . . Ngati inu simukulikhulupirira ilo, khalani kutali kwa ilo; ilo lidzakuvulazani inu. Koma ngati inu mukukhulupirira ilo, mukhale nalo ilo, ilo lidzakutengerani inu ku chigonjetso, motsimikiza basi monga dziko lapansi.

39 Tsopano ife tikupeza, kuti, "Abrahamu sanadzandime pa lonjezo la Mulungu." Ndipo pamene iye anali usinkhu wa zaka handiredi, ndipo mkaziyo anali nainte, ine ndikukhoza kumumva iye; sakutha kuyankhula tsopano, iye akukalamba komanso akufooka, "Chabwino, Sarah, wokondedwa, iwe ukumva bwanji?"

"Chabwino, wokondedwa, ine sindikumva kusintha."

40 "Aleluya! Ndife—ife tikhala naye iye, mulimonse. Mulungu ananena chomwecho, ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo. Mulungu anapereka lonjezo." Iye anati iye anali "wokakamizidwa kwathunthu kuti Mulungu anali wokhoza kuchita zimene Iye analonjeza."

41 Ndipo tsopano ife timadzitcha tokha Mbewu ya Abrahamu, Mbewu yake Yachifumu (osati mbewu ya Isaki), Mbewu yake Yachifumu, Khristu; ndipo nkumazandima pa lonjezo lirilonse, kukangana nalo ndi kunena kuti izo si choncho, ndi kukayikira izo mmalingaliro athu? Ine ndikukayika ngati ife tiri Mbewu ya Abrahamu pamene ife tiri nalo lingaliro la mtundu umenewo mwa ife. Mbewu ya Abrahamu siyinadzandime pa kalikonse. Iyo imatcha zinthu zomwe panalibepo, ngati kuti izo zinalipo, chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Iye ndi Mlengi. Iye akhoza kuchipanga icho chomwecho. Iye analonjeza izo, ndipo izo zikukhazikitsa izo. Ndizo zonse zomwe zilipo kwa izo. Pamene Mulungu anena zimenezo, izo zimakhazikitsa chinthu chonsecho. Tsopano, kumbukirani, iye ankazifuna izo. . . Apo sipakanakhoza. . . Iye anamuuza. . .

42 Chinthu china chimene Iye anamuuza iye kuti achite, kuti adzipatule yekha tsopano kwa abale ake ndi anthu ake onse.

43 Mulungu, kuti amutenge mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, kuti azimumvera Iye, iwe uyenera kudzipatula wekha ku kusakhulupirira konse, ndiko kulondola, kufikira iwe utadzilekanitsa wekha kwathunthu kwa chirichonse chosiyana ndi Mawu amenewo, ndi kuwakhulupirira Iwo. Inu . . . Mulungu amaitanira ku kudzilekanitsa kwathunthu.

44 Ndi kusiyana kotani kumene kulipo lero mu masukulu athu amene akutumiza atumiki. Iwo amangowadzadzitsa iwo ndi mitundu yonse ya kusakhulupirira ndi malingaliro omwe salinso Mwamalemba kuposa mtundu wina wa kachikhulupiriro kamene iwo amapanga, ndiyeno nkuwatumiza iwo kunja ndi maziko otero monga amenewo. Nzosadabwitsa ife taswa gulu la Oswald ndi Jack Ruby, ndi ena otero, kudutsa mdzikoli. Chikominisi chikulimeza dzikoli, chifukwa ife tiri ndi maseminare ndi alaliki ofungatiridwa mmalo mwa otumidwa ndi Mulungu, obadwa-mwatsopano, odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ana a Mulungu obadwa ndi Moto, ana a Abrahamu amene amakhulupirira Mawu a Mulungu kuti ndi Choonadi chotsimikizika ndipo palibe china koma Choonadi, wolimba, ndipo akhoza kuyima pamenepo pa malonjezo, pamaso pa chirichonse, ndi kuyang'anizana nazo izo, kuti izo ndi Choonadi. Ndi Mawu a Mulungu. Chabwino.

45 Tsopano Iye anati, "Udzipatule wekha kwa abale ako onse, kwa anthu ako onse, chirichonse, ndipo unditsate Ine."

46 Mulungu sanasinthe njira Yake. Mulungu ndi Mulungu wosasinthika. Momwe Mulungu amachitira chirichonse, nthawi ina, Iye ayenera kuti achite icho mwanjira yomweyo kachiwiri. Kumbukirani, pamene mungakhoze kuwona zochita za Mulungu nthawi iliyonse, ngati Iye . . . Ngati—ngati munthu anatayika, ndipo Iye anamupulumutsa munthu pa maziko a lingaliro lina lirilonse limene Iye anapanga, Iye ayenera nthawizonse kukhala ndi chisankho chomwecho. Iye sangakhoze kuchisintha icho. Mukuona? Iye ndi wopandamalire.

47 Ife ndife amalire. Ine ndikhoza kudziwa zambiri mawa kuposa momwe ndikudziwira lero. Kotero inu mukhoza kudziwa zambiri chaka chamawa kuposa momwe inu mukuchitira chaka chino. Inu mukudziwa zochuluka chaka chino kuposa momwe munachitira chaka chatha, koma osati Mulungu.

48 Iye ndi wangwiro, wopandamalire. Chirichonse chimene Iye amachita ndi changwiro. Iye sangakhoze kupanga lingaliro lero ndi kupanga labwinoko mawa. Loyamba Lake limakhala langwiro. Chotero, inu mukhoza kungopachika moyo wanu pa chirichonse chimene Iye anena, icho ndi Choonadi.

49 Mulungu anaitanidwa pa nthawi imodzi kuti apange chisankho, momwe angamupulumutsire munthu, ndipo momwe Iye anachitira izo zinali pa maziko a Magazi okhetsedwa a Mmodzi wosalakwa, mmunda wa Edeni. Ndipo munthu

wayesetsa chirichonse mdziko kuti amupulumutse munthu, mwinamwake; iwo amanga mizinda, iwo amanga nsanja, iwo akhala nawo mabungwe, maphunziro, ndi china chirichonse, ndipo chinthu chonsecho ndi kulephera kwathunthu. Ilipo njira imodzi yokha imene Mulungu amapulumutsira konse munthu, ndiyo kudzera mu Magazi okhetsedwa a Wosalakwa. Ndiyo njira yokhayo. Chimenecho chinali chigamulo choyamba cha Mulungu. Iye amakhalabe ndi icho nthawizonse.

50 Ngati Mulungu anamuchiritsapo munthu pa maziko amene Iye anamuchizira iye, Iye ayenera kumuchiza winayo pamene iye abwera pa malo amenewo. Ngati Iye satero, Iye anachita molakwitsa pamene Iye anachita nthawi yoyamba pamene chigamulo chinali choti chipangidwe.

51 Ngati Iye apanga konse chigamulo, Iye ayenera kukhala nacho icho nthawizonse. Ngati Iye satero, Iye anapanga lingaliro lolakwika pamenepo. Mukuona? Ndipo ndani anganene kuti Mulungu anapanga chigamulo cholakwika? Mukuona? Ife sitingakhoze kunena zimenezo. Kotero Mulungu ayenera kukhalabe ndi lingaliro Lake. Kotero pamene Iye apanga ilo, ndi limenelo.

52 Kotero iye anati, "Udzipatule wekha kwa abale ako onse, chirichonse, kusakhulupirira konse kumene kunabwera kumeneko kuchokera ku Babeloni kumtunda uko."

53 Gulu loyamba lalikulu padziko lapansi linali Babulo, pamene ilo linapanga bungwe mizinda yonse kuti ilipire msonkho kwa mzinda umodzi uwu, choimira kumene, timalingaliro tonse iti ndi zinthu zatsopano zomwe zikuwoneka lero. Ngati inu munayamba mwawerengapo *Two Babylons* la Hislop, ndi zina zotero, ndi kubwerera mu Genesis, inu mukapeza kuti Genesis ndi chiyambi, mbewu, inu mukawona timalingaliro tonse iti ndi zinthu, molondola titayikidwa pomwe apo.

54 Mwaona, Afarisi odzitukumula okha amene anatsika kuchokera kumeneko, kuchokera kwa mkazi ameneyo ali ndi mizu yodabwitsa iyo ndi zina zotero, anabwera kumeneko mmasiku a Yesu. Afarisi samakhulupirira mu Mzimu kapena china chirichonse, ndipo iwo ankamutchinga Yesu. Yesu anati, "Asiyeni iwo okha. Ngati wakhungu atsogolera wakhungu, iwo awiri onse adzagwera mu dzenje. Mulole. . . " Iye anapitirizabe kulalikira, ndi kuchiritsa odwala, ndi kuchita zozizwitsa, ndipo chimodzimodzi basi. Izo sizinamuletse Iye, chifukwa Iye anali Mawu. Mawu amapitirirabe, mosalabadira zimene zingachitike.

55 Kotero ife tikupeza zinthu zimenezo zikupitirira, ndipo izo potsiriza zinadzafika pa kuphuka kuno mmasiku otsiriza. Monga Yambre ndi Yane anamutsutsa Mose, kotero izo zidzakhala chinthu chomwecho.

56 Tsopano, kudzilekanitsa kwathunthu ku kusakhulupirira konse. Ndipo, kumbukirani, Abrahamu mbadwa sanadalitsidwe kwathunthu mwamtheradi mpaka iye atamvera ndendende zomwe Mulungu anati achite. Ndipo ife sitidzatero, konse, sitidzadalitsidwa konse, ndi kudzakhala ndi madalitso, mpaka ife titadzamvera chimene Mulungu anati tichite.

57 Chinthu china chimene ine ndikufuna inu muchizindikire apa mu mutu wa 12, kuti pangano linali palimodzi lopanda mangawa. Apo panalibe chirichonse cholumikizidwa kwa ilo. "Ine ndatero," osati "ngati inu." Apo panalibepo ma ngati kwa ilo. "Ine ndachita kale izo." Iye anamupatsa Abrahamu pangano, lopandamangawa.

58 Ndipo tsopano dziwani, mu pangano la Adamu, ilo linali, "Ngati iwe sudzawukhudza mtengo uwu, ndiye Ine ndidzachita *chakuti-ndi-chakuti*. Koma ngati inu mutero, ndiye ine ndiyenera kuchita *zakuti-ndi-zakuti*." Mwaona, ilo linali ndi lamulo lolumikizidwa kwa izo.

59 Koma mu pangano ili, "Ine ndakupanga kale iwe atate wa mafuko ambiri." Ndipo Iye ali-. . . Zonsezo ndi zopanda mangawa. Panganolo ndi chisomo changwiro, basi mwantheradi chisomo. Chinthu chokhacho chimene iwo ankayenera kuchita kuti asunge pangano ili chinali kukhala ndi kumakhala mdzikolo; ndipo mdalitso uliwonse, umapita ndi panganolo, linali ndi iwo. Chinthu chokha chimene iwo ankayenera kuchita chinali kukhala mdziko limenelo. Tsopano ife tikupeza kuti, pamene iwo anapita uko ku Igupto, iwo anataya mdalitso wawo, koma osati pangano lawo. Pangano linali liripobe pamenepo. Iwo anataya mdalitso, koma osati pangano lawo, chifukwa pangano lawo linali chisomo, mopandamangawa.

60 Ndipo mu—mu Eksodo, mutu wa 19, Ek-. . . Israeli anapanga chimodzi cha zinthu zake chopupuluma kwambiri chimene iye anayamba wachitapo, chinali pamene iwo anakana chisomo ndi kulandira lamulo. Taonani chimene chisomo chinali chitachita. Chisomo chinkayenera kuwapatsa iwo wowombola, chinayenera kuwapatsa iwo mneneri, ndi Lawi la Moto kuti limutsimikizire iye ndi Mawu otsimikiziridwa, anali mwanawankhosa wansembe. Chisomo chinali chitawapatsa iwo chitsitsimutso chachikulu. Chisomo chinali chitawabweretsa iwo kudutsa, chinatsegula Nyanja Yofiira, chinawabweretsa iwo kuti awoloke pamenepo. Chinawapulumutsa iwo ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, zonse mwa chisomo. Koma iwo ankafuna chinachake kuti adzipangire okha maina akuluakulu.

61 Tsopano, ngati amenewo siali anthu lero, ndi chinthu chomwecho basi. Iwo ayenera kukhala, munthu ayenera kuti adzitengere yekha kukhudzidwa mu zimenezo penapake. Ndipo apo ndi pamene Israeli anapanga kulakwitsa kwake kwakukulu, pamene iye anakana chisomo ndikutenga lamulo, mmalo mwake.

Ndipo a. . . Komabe, koma pangano limene Iye analipanga ndi iwo linali lopandamangawa. Icho chikadali chinthu chomwecho lero, ife tikuchipeza icho.

62 Abrahamu, ndiye, iye atatha kupatsidwa ziyeneretso izi, iye anayamba ulendo wake, kumapitirira. Tsopano ife tikupeza kuti iye anasunthira kunja.

63 Ndipo mu mutu wa 13, iye potsiriza anafika pa malo a kumvera kwathunthu kwa Mulungu. Tsopano ife tikupeza, mu mutu wa 13, kuti Loti. . . Choyamba, iye anatenga bambo ake, ndipo bambo wokalambayo anali nthawizonse wokoma mu njirayo. Ndipo iye anayesetsa kutenga gulu likukokera limodzi ndi iye. Ndipo pamene inu muchita zimenezo, apo ndi pamene inu munazipeza zimenezo. Mulungu anati, "Dzilekanitse."

64 "Chabwino, ine ndikukuuzani inu, iwo samakhulupirira ndendende, koma. . ." Ndiye amachokako kwa izo. Ndicho chinthu chokhacho, ingokhalani kutali ndi izo.

65 Ndiyeno munthu wokalambayo, iye potsiriza, iwo atamuika iye, ndiye, Loti anakhala a—tsitsi mu bisiketi, monga kunena kwake. Ife tikupeza kuti iye anayamba kung'ung'udza. Ndipo awiri onse analemera, ndipo iwo anali nazo zochuluka zoti azigwirizana nazo. Ndipo ife tikupeza ndiye kuti Loti anayamba kukangana, olishya ake kutsutsana ndi olishya a Abrahamu.

66 Ndipo ife tikupeza kuti Iye analibe, Mulungu anali asanapeze kukhulupirika kwathunthu. . .-aham, Abraham, kumvera zimene Iye anamuuza iye kuti achite, kudzipatula kwathunthu kwa abale ake onse, kuchoka kwa anthu ake onse, ndi kukamtumikira Iye.

67 Kotero ife tikupeza kuti, Mulungu akuyankhula ndi Abrahamu apa, pa guwa, ndipo anali atamuuza iye choti achite. Potsiriza, Loti, pamene panadzabwera funso pakati pa Abrahamu ndi Loti; anali mwana wa m'bale wake Harani, ndipo iwo. . . Iye akanakhala mdzukulu wake. Ndipo potsiriza anati, "Tiyeni. . . Ndife abale tsopano. Ife sitikhala ndi mikangano iliyonse pakati pathu. Tsopano inu, ngati inu mupita kummawa, ine ndipita kumadzulo. Ndipo ngati inu mupita kumadzulo, ine ndipita kummawa. Tsopano inu tingodzilekanitsa tokha, ndipo ife sititero. . . Pali malo okwanira apa a ife tonse. Ndipo inu muzingopita, inu mungopanga kusankha." Tsopano umenewo unali mzimu weniweni wa Chikhristu mwa Abrahamu, anamupatsa ngakhale mdani phindu la kusankha. Ndipo kotero iye anamulola iye atenge njira yake.

68 Ndipo Loti, monga ochuluka kwambiri lero, anawona mwayiwo. Ngati iye anayamba wachoka ku kusamalitsa uko, bwanji, iye akhoza kudzipangira yekha madola angapo, iye akhoza kukhala munthu wotchuka. Kotero iye anayang'ana pansi cha ku Sodomu. Ndipo ilo linali dziko lothiriridwa bwino, ndi mzinda wawukulu, ndi makampani akulu a mchere, ndi

zina zotero. Iwo, iwo anali nazo zokagulitsa kwina kuchokera kumeneko. Ndipo—ndiyeno, kachiwiri, iwo unali wodzaza ndi nthawi yaikulu, akazi ndi utoto wawo wonse wa Yezebeli ndi chirichonse, nthawi yopambana basi. Mkazi wake anakhala ngati ankamverera choncho, nayenso, chifukwa, ife tikupeza kuti, iye anadzakhala meya kumusi uko komwe iye ankakhala ngati—iye ankakhala ngati ankakonda njira ya anthu. Ndipo ndicho chinthu chokhacho chimene inu muyenera kuchita, ndi kusakanizikana ndi chinachake. Mukuona?

69 Mulungu akufuna kuti inu mudzilekanitse nokha, ndipo—ndipo mukhale kutali kwambiri ndi zinthu zimenezo mpaka inu osamaziwona izo nkomwe. Kuti, inu mukufuna kuwona chinthu chimodzi, ndicho Iye ndi chimene Iye analonjeza.

70 Koma Akazi a Loti, iwo anakhala ngati anazikonda zimenezo. Ndipo, sindikukaikira, iye anakhala ngati anati, "Wokondedwa, tsopano ine ndinali uko, ndipo iwe ukuwona momwe akazi akuvalira kumusi uko, ndipo tayang'ana pa atsikana amenewo. Tayang'ana mmene atsikana athu akuvalira. Chotero kodi iwe sukuganiza kuti iwo ndi amakono mochuluka?" Oh, mai! Ngati ife sitinabwerere ku Sodomu wina, ine sindikudziwa chifukwa chake. Apo ife tikupeza.

71 Koma Abrahamu anakhala ndi lonjezo. Ndiye ife tikupeza kuti, pamene izo zikupitirira, ndi...pamene iwo anadzilekanitsa okha, ndi Loti. Ndipo Abrahamu anatenga malo osawukawo, njira yaying'ono, anakakhala kumeneko kumene kunalibe msipu wambiri wa ng'ombe zake. Ndipo, koma, iye anali wokonzeka kutenga njira, chifukwa Mulungu anali atamuika iye mdziko limenelo, ndipo ndi kumene iye ankafuna kuti azikhalako. Anakonzeka kuti alitenge ilo.

72 Tsopano pamene pomalizira pake, anamumvera Mulungu kwathunthu, pamene pomalizira pake anamumvera Mulungu ku chidzalo chake, kuti adzilekanitse yekha kotheratu, panali pamenepo ndiye Ambuye anawonekera kwa iye kachiwiri. Kufikira atachita zimenezo, Ambuye anakhala kutali ndi Abrahamu. Koma pamene iye anamvera kwathunthu, ndiye Loti...Mulungu anawonekera kwa iye, Iye anati "Abrahamu, kweza maso ako mmwamba. Yang'ana kum'mawa, yang'ana kumadzulo, yang'ana kumpoto, yang'ana kum'mwera, zonse za izo ndi zako." Ameni. Tsopano, ine ndikuzikonda zimenezo.

73 Ndipo, inu mukudziwa, icho ndi chinachake chonga chinali pamene ine ndinapulumutsidwa. Ine nthawizonse ndinkamva za Mulungu kukhala Mulungu wamkulu. Ndipo, inu mukudziwa, pamene ine ndinapulumutsidwa, ine...Winawake anati, "Tsopano zonse zimene inu muyenera kuchita ndi kujowina mpingo, ndi kuyika dzina lanu pa mpukutu wa mpingo uwu kuno ku mpingo wa Baptisti. Ndizo zonse zomwe inu muyenera kuchita."

74 Koma, inu mukudziwa, tsiku lina ine ndinawona kuti ine ndinali wolandira cholowa cha chinachake, mwakuti ine—ine—ine ndinkafuna kuti ndiyang'ane mopyoza icho ndi kuwona chimene ine ndinali nacho. Inu mukudziwa, ndine basi wa choncho. Monga a—chinyumba chachikulu, iwe ndi chako, ndipo—ndipo chirichonse chimene chiri mmenemo ndi chako.

75 Iwe—iwe sumadziwa zomwe uli nazo mpaka utapita kuti ukayang'ane kudutsa mu Baibulo, kuti ukapeze malonjezowo. Ameni. Iwo angakutchingire iwe kwa izo ngati iwo angathe; koma izo ndi zako. Lonjezo lirilonse ndi la kwa Abrahamu ndi kwa Mbewu yake ya pambuyo pake. Ameni. Lonjezo Lauzimu lirilonse mu Mawu ndi la Abrahamu ndi Mbewu yake, ndipo ndinu olandira a ilo. Wolandira! Oh, mai! Ine ndimakonda kuyang'ana mmenemo kuti ndiwone zomwe ine ndiri nazo. Ngati winawake andipatsa ine chinachake, ine ndimakonda kuchiyang'ana icho. Ndipo ine ndimakonda kuyang'ana mu Baibulo ndi kuwona chimene chiri changa. Mbewu iliyonse ya Abrahamu iyenera kumachita zimenezo, pamene iwe ubadwa mwatsopano, wadzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo Mzimu Woyera uli pa iwe, ndiwe wolandira ku lirilonse la malonjezo amenewo.

76 Inu mukudziwa, ziri monga ine ndinanenera, chinyumba chachikulu, pakuti ife timabatizidwa kulowa mchinyumba chimenecho. Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndipo Thupi limenelo ndi Khristu, amene ali Mbewu Yachifumu ya Abrahamu, ndi olandira kwa chirichonse chimene chiri mmenemo. Ameni. Chirichonse chimene chinali mwa Mulungu, Mulungu anachitsanulira mwa Khristu; chirichonse chimene chinali mwa Khristu, Iye anachitsanulira mwa wokhulupirira. Ameni. Mulungu pamwamba pathu, Mulungu ali nafe, ndi Mulungu mwa ife! Chirichonse, lonjezo lirilonse la mu Bukhu, ndi lanu ngati inu mungalikhulupirire ilo, ngati inu muli nacho chikhulupiriro chokwanira kuti muvomereze izo ndi kuzikhulupirira izo.

77 Inu mukudziwa, ine ndimayang'ana pozungulira, ngati ndipeza chinachake chimene chiri chokwera kwambiri, ndimadabwa chomwe chiri mmenemo, ine ndimadzipezera makwerero ndi kuwakankhira iwo pamenepo, ndi kumapitiriza kukwera mpaka ine nditafika kwa icho. Imeneyo ndiyo njira yake, lonjezo la mu Baibulo, ngati chirichonse chiwoneka ngati chiri chodabwitsa kwa ine, Ine ndimangopitirira kumapemphera mpaka ine nditachifikira icho. Ndizo zonse. Ndiyo njira yake yochitira izo. Zipitirirani kupemphera, zipitirirani kumagwiritsitsa, kumakwera mmwamba, kumakhulupirira, mpaka mutadzakhala. . .Ndinu olandira wa izo, inu muli nalo lonjezo kwa izo, ndipo inu muli nawo ufulu kwa izo, ndipo, "Pemphani ndipo mudzalandira, pakuti zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira."

78 Tsopano ife tikupeza kuti Abrahamu anayenda kudutsa dzikolo. Mulungu anamuuza iye, anati, "Yenda kudutsa mdzikoli, yang'anani pamwamba pake. Chirichonse muno ndi chako. Chidutswa chirichonse cha ilo ndi chako. Izo zonse ndi zako."

79 Tsopano ife tikupeza ndiye, kuti, kuti mu mutu wa 14 wa Eksodo tsopano kapena. . .Mutu wa 14 wa Genesis, mundikhulululukire ine. Mu mutu 14 wa Genesis, Abrahamu ndi Loti anali atalekanitsidwa, ndipo Loti pomalizira pake analowa mu vuto lina. Ndipo inu nthawizonse mudzatero, pamene inu mudzilekanitsa nokha kwa okhulupirira, inu mudzalowa mu vuto. Ife tikupeza kuti mafumu anachita chitaganya ndipo iwo anapanga nkhondo. Ndipo iwo anabwera kumeneko ndipo anatenga Sodomu, iwo anatenga Gomora, iwo anatenga mafumu awo onse a ku zigwa ndi zigwa, ndi chirichonse, ndipo anamutenga Loti. Ndipo anthu ochepa okha ndi amene anathawira kumapiri.

80 Ndipo pamene iwo anatero, winawake amene anathawa anabwera ndipo anadzamuuza Abrahamu Mhebri, anati, kuti, "Sodomu wagwa, ndi Gomora, ndipo iwo atenga mafumu ake, ndi—ndi zina zotero, ndipo atenga anthu onse, ndi zakudya zawo, ndi chirichonse chimene iwo anali nacho. Ndipo amutenga Loti ndi mkazi wake, ndi ana ake aakazi, ndi akazi onse, ndipo apita nawo iwo."

81 Tsopano, Abrahamu, penyani mzimu wa Chikhristu uwu ukumulondola m'bale wake. Ngakhale kuti, ngakhale, Loti anabwerera mmbuyo, anabwerera mmbuyo, komabe Abrahamu ankamukonda iye. Iye anapitirirabe kumamutsatira.

82 Chimodzimodzi monga Yesu, mu M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Komabe, iwo anamuchotsa Iye mu mpingo wawo. Ndipo Iye anali kunja, akugogoda, kuyesetsa kuti abwerere mkati. [M'bale Branham akugogoda pa guwa—Mkonzi]. Ngati Iye akanangopeza winawake kuti atsegule chitseko kuti Iye akhoze kulowamo!

83 Apo pali mzimu umenewo wa Abrahamu, mwaona, ukumutsatira m'bale wake wakugwa, wotsitsidwa. Ndipo iye anamutsatira iye, ndipo anatenga antchito ake achimuna firii handiredi ndipo anawapatsa zida. Ndipo iye anakomana naye ku Dani; ndiwo mapeto otheratu a Palestina kumeneko. Ndipo iye anakomana naye iye kumeneko, ndipo anadzilekanitsa yekha usiku, ndipo anawalondola ndipo anamenyana ndi ankhondo kumusiko, ndipo anagonjetsa mafumu, ndipo anawapha iwo, ndipo anabweretsa onse amene anatulutsidwa kunjako.

84 Zindikirani, pamene iye anabwerako, ndi chithunzi chokongola bwanji apa. Ndi chifukwa chake ine ndimangokonda kuwoneratu izi pang'ono, kotero ife tikupeza. . .ine ndisanafike ku mutu wanga wa *Yehova-Yire*. Ngati inu mungazindikire

Abrahamu akubweretsa zonse zimene zinali zitatayika, m'bale wake wosochera ndi ana, pamene iye ankawabweretsanso iwo, mafumu anatuluka kuti adzakomane naye iye.

85 Ndipo Melkizedeki anatuluka, "Amene anali Mfumu ya Salemu, Mfumu ya mtendere, Mfumu ya chirungamo, Mfumu ya Yerusalemu; wopanda bambo, wopanda amayi, wopanda chiyambi cha masiku, wopanda mathero a moyo." Melkizedeki anakumana naye iye pa kup-. . .akubwera kuchokera kokapha mfumu, kwa Yemwe mbadwa Abrahamu (Ahebri 7) anakumana naye Munthu uyu ndipo anapereka chakhumi, chakhumi. Ndi munthu wamkulu bwanji ameneyu ayenera kuti anali! Inu mukuganiza iye anali ndani? "Iye analibe bambo. Iye analibe amayi. Iye sanachite kuyamba." Ndipo yense Yemwe Iye ali, Iye akadali wamoyo. "Iye sanathe konse. Mfumu ya Salemu, Mfumu ya mtendere!" Oh, anali Ndani Munthu wamkulu uyu?

86 Ndipo zindikirani choyimira chomwe ife tikuchipeza apa. Nkhondo itatha, atatha wo—wokhulupirira weniweni kumenyana ndi mdani, anaswa mizereyo ndipo anayesetsa kuti amugwire m'bale wake, Mbewu yeniyeni ya Abrahamu kumubwezera m'bale wosocherayo, Melkizedeki anatulukira ndipo anaperekera vinyo ndi mkate, mgonero, kupereka mgonero nkhondo itatha, anaperekera mgonero kwa iye itatha nkhondoyo.

87 Choyimira chokongola kwambiri cha pamene nkhondo idzatha, kuno pa dziko lapansi, zigonjetso zapambanidwa. Yesu anati, "Iwo adzadya iwo mwatsopano mu Ufumu wa Atate," wosocherayo atatha kubwezeretsedwa. Ndiye chinthu choyambirira chimene ife timachita pamene ife tipita mmenemo, nkhondo itatha, ndi kukakhala pansi pa gome mu Ufumu wa Mulungu. Ndipo kumeneko iwo amene anamenyera, ndipo akhala pansi ndi kulakika, adzavekedwa mu chirungamo cha Khristu, ndiyeno kenanso iwo anatenga mkate ndi vinyo, mu Ufumu wa Atate kumbali inayo. Ndi chithunzi chenicheni bwanji ichi, cha Abrahamu akutuluka ndipo akumutenga Loti ndipo akumubweretsanso iye.

88 Tsopano ife tikupeza ndiye, kuti mu mutu wa 15, ife tikupeza chinachake chapadera kwambiri apa. Ine—ine ndikukhala ngati ndikuzikonda izi, mwabwino kwambiri, powona yemwe Abrahamu anali tsopano, ndipo Abrahamu ndi Mbewu yake pambuyo pake. Ife tikupeza apa, kuti Abrahamu atatha kuchita zinthu zonse zazikulu izi; kukhulupirira Mulungu, kugwiritsitsa ku lonjezano, kudzilekanitsa yekha, ndipo nthawi zonse kumatsatira njira ya—ya kusunga malamulo a Ambuye; ife tikupeza kuti Mulungu anawonekera kwa iye pa guwa. Ndipo Abrahamu anamufunsa Iye funsolo, iye anati, "Tsopano, wolandira cholowa changa ndi ndani koma—koma Elieza uyu wa ku Damasiko? Ndipo tsopano Inu munandilonjeza ine Mbewu.

Ndipo ine—ine ndikufuna kuti Inu muchite chinachake; ine ndikufuna kuti Inu mutsimikizire lonjezo ili kwa ine."

89 Ndipo Mulungu ananena kuti Iye akanadzatsimikizira izo kwa Abrahamu, kutsimikizira pangano limene Iye anali atalipanga pakati pa Iye ndi Abrahamu. Tsopano Iye amupatsa iye chizindikiro kuti izo zikhala zoona. Kuti, ngakhale iye ali wokalamba, iye ali pafupifupi eyite-faivi tsopano, komabe Iye adzatsimikizira kwa iye, mwa chizindikiro, kuti Iye asunga pangano limenelo.

90 Oh, ndine wokondwa kwambiri kuti Mulungu nthawizonse amatipatsa ife zizindikiro, chifukwa Iye . . . Ife tiyenera kudziwa, lero, kuti ora limene ife tiri nkukhalamo tsopano, pakuyenera kukhala chizindikiro pa dziko lapansi pa nthawi ino. Ife tiyenera kuyang'anira chizindikiro chimenecho. Mulungu samachita konse kalikonse popanda poyamba kuwapatsa anthu chizindikiro ndi chenjezo. Ndipo chizindikiro chenicheni chimatsatiridwa ndi liwu, ndipo liwu nthawizonse limakhala liwu la Mwamalemba.

91 Tsopano Iye atsimikizira pangano kwa Abrahamu, kapena Abramu, apobe. Ndipo Iye anati, "Tenga iwe mwana wang'ombe." Tsopano, kumbukirani, pali mwana wang'ombe wamkazi. "Ndipo utenge mbuzi yaikazi ya zaka zitatu. Iliyonse iyenera kukhala ya zaka zitatu." Zindikirani, ng'ombe ya zaka zitatu, yaikazi; mbuzi ya zaka zitatu, yaikazi. "Ndi nkhosa," yaimuna. Iliyonse zitatu, zaka zitatu, ndipo pali atatu a iwo. Atatu; zazikazi, ziwiri, ndi yaimuna. Mukuona? Wazaka zitatu, nsembe yoyera, mwanawankhosa . . . ng'ombe yamphongo, mbuzi yaikazi ya zaka zitatu, kenako nkhosa yamphongo.

92 Ngati mungazindikire, chirichonse kumeneko chikumanga kukhala chizindikiro. Ndipo tsopano ine sindikuyenera kulalikira chiphunzitso kuchokera pa nsanja pano, ndipo ine ndikutsimikiza iwo apafupi mokwanira mukukhoza kuziwona. Zindikirani. Ndipo anatenga ziwiri, mbalame ziwiri. "Wina njiwa ndi wina nkhunda," zomwe ziri za banja limodzi, njiwa ndi nkhunda.

93 Tsopano iye anayidula mbuzi . . . nkhosa pawiri. Iye anadula—nkhosa ndi mbuzi, ndi zinazo. Iye ankaziganga izo, kuzidula izo pakati, ndipo ankazigoneka izo pansi. Koma nkhunda, iye . . . ndi njiwa, iye sankaziganga. Zinali zimenezo, ndithudi, aliyense amene amadziwa Lemba, akudziwa kuti awo ndi machiritso Auzimu. Mwaona, izo ziri mu mapangano onsewo. Ndipo kotero ife tikupeza, iye ankaziyika izo mkati. Machiritso nthawizonse amakhala mwa chikhulupiriro mu Magazi okhetsedwa, nthawizonse. Ndipo pangano lakale linali ndi machiritso Auzimu, ndi mochuluka bwanji Pangano Latsopano liri nawo iwo? Mukuona? Ngati pangano lakale linatulutsa iwo, nanga bwanji Latsopano, pamene, "Ndiro

pangano labwino kwambiri, kuyankhula za zinthu zabwino, zapamwamba, zazikulu, zabwinoko"? Pangano Latsopano!

94 Tsopano ife tikupeza mu izi, kuti Abrahamu, pamene iye anachita izi, ndiye zindikirani chimene chinachitika. Tsopano apa pali mfundo yabwino, yopambana. Ine sindikufuna kuti inu mu—mu—muiphonye iyo. Kutsimikizira kwa pangano, mwa kuyankhula kwina, ndi lonjezo, kuti, "Ndine woona pa zomwe Ine ndimachita kapena zomwe Ine ndikunena kuti Ine ndichita," Mulungu akutsimikizira izo kwa Abrahamu.

95 Ndipo iye anatenga nsembe zimenezo ndipo anazipha izo, ndipo anakaziyika izo kumapeto ndi mapeto, pamodzi, pamene ankazigoneka izo; ndipo ankayingitsa mbalame kuti zisabwere pamenepo, kuchitira kuti mbalame zisabwere pa nyama yatsopanoyo, mpaka dzuwa litalowa, madzulo. Ndipo pamene dzuwa linalowa, kapena linali likulowa, apa Iye ankamuwonetsa Abrahamu zimene Iye ati adzachite m'tsogolo, zimene zinali zoti zidzachitike.

96 Zindikirani, Iye anamuuza Abrahamu: Chinthu choyamba chimene iye anachiwona chinali chowopsya chenicheni cha mdima chimene chinadza pa iye. Choyamba, tulo tatikulu kwenikweni tinamugwera iye. Tsopano, tulo limenelo linkaimira imfa kwa anthu onse. Munthu aliyense ayenera kufa; imfa kwa anthu onse. Tulo limenelo linabwera pa iye; ndipo izi zisanachitike a—a—kuwopsya kwenikweni kwakuda; ndipo kenako panapita ng'anjo yamoto; ndipo zitatero Kuwala kwakung'ono koyaka kunapita pakati pa panganolo, kunapita pakati pa nsembezo, kunagawaniza izo. Tsopano kodi zimenezo zikutanthauza chiyani? Izo zikutanthauza kuti munthu aliyense ayenera kufa; ndipo kwenikweni, zitatha zimenezo, ayenera kupita ku gehena; ndiko kulondola, mu mdima, mdima wakunja, kulekanitsidwa ndi Mulungu; koma Kuwala kunabwera mkati, ndipo kunadzalowa pakati, kugawaniza nsembe zimenezo. Ngati inu mukumvetsa, ife . . . Pangano limenelo!

97 Monga ife Achimereka, ife timapanga bwanji pangano? Chabwino, chinthu choyamba chimene ife timachita, ife timati, ife tipanga mtundu wina wamalonda kapena chinachake, ife nthawi zambiri timapita kunja ndi kukadya; ndi kukakhala pansi, kukayankhula kwa kanthawi, ndipo zikatero timadzapereka malingaliro athu; ndiyeno nkudzagwirana chanza wina ndi mzake. Ife timati, "Gwirani pa izo!" Ndiro pangano lathu. Ndiro lonjezo lathu.

98 Tsopano, ku Japan, inu mukudziwa momwe iwo amapangira pangano ku Japan? Iwo amakhalanso ndi chinachake choti adye; akatero iwo amatola botolo la mchere, ndipo amaponyerana mchere pa wina ndi mzake. Ndiko kutsimikizira kwa panganolo.

99 Ife timagwirana chanza, ndikuti, "Ndi zosindikizidwa, mnyamata wakale. Ine ndikukhulupirira izo. Ine ndikhala ndi

iwe. Ndiro lonjezo."

100 Ku Japanese, Japan, iwo amaponyerana mchere pa wina ndi mzake. "Zasindikizidwa, bwanawe. Ndiko kutha kwa izo." Ndiko kutha kwa mikangano yonse zikatero. Iwo, iwo amapanga pangano, amatsimikizira izo, poponyerana mchere wina ndi mzake.

101 Koma mmasiku akale. . .(Kodi ndingatenge chimodzi cha izi?) [M'bale Branham akutenga kachidutswa ka pepala—Mkonzi]. Mmasiku akale, umu ndi mmene iwo ankapangira pangano. Ife tinkapanga mgwirizano, ndipo ife tinkatenga mgwirizanowo ndi kulemba iwo monga *chomwecho*. Ndiyeno ife tinkapha nyama, nsembe; tinkaiganga iyo, tinkaiyika iyo monga zinkakhalira mu nthawi ya Abrahamu kumeneko. Ndiyeno ife tinkayima pakati pa pangano ili, inu ndi ine, ndipo ife tinkalumbira kwa Mulungu. "Ngati ife tilephera kusunga pangano ili, mulole ife tidzakhale monga nsembe yakufa iyo imene inafa m'malo mwathu. Tiyeni magazi a nsembeyo adzayankhe pa ife. Ifenso tidzafe imfa yomweyo, ngati ife tidzalephere kusunga pangano."

102 Ndiye zonsezo zinkalembedwa pamenepo, kapena zinkalembedwa pa kachidutswa ka pepala monga *choncho*. Ndiye iko nkakang'ambidwa pakati, monga *choncho*. [M'bale Branham akung'amba kachidutswa ka pepala pawiri—Mkonzi]. Tsopano iwe utenge theka limodzi, ndipo ine nditenge theka. Ndipo tsopano, inu mwaona, iwe sungakhoze kubwereza izo nkomwe, makamaka pamene izo zalembedwa pa chikopa cha nkhosa. Mwaona, iwe sungakhoze kuchibwereza icho nkomwe. *Ichi* chiyenera kugwirizana ndendende ndi *icho*, kuti zikhale chomwecho. Ndiyeno pamene ife tibwera pamodzi, ine ndikunyamula gawo limodzi, inu mukunyamula gawo linalo. Ndiyeno pamene ife tibwera pamodzi, ndipo pangano ili liyenera kupangidwa, ndipo malumbiriro athu ayenera kuperekedwa, ndiye chidutswa cha pepala langa chiyenera kugwirizana ndendende ndi chidutswa cha pepala lanu, ndipo kotero inu ndinu amene muli ndi ine mu pangano.

103 Chimene Mulungu anali kusonyeza pamenepo kuti Iye anali kuchita, kuti Mulungu Mwiniwake anali kubwera pansi kuti adzapangidwe thupi, ndipo Iye anali woti adzakhala mu pangano. Ndipo Mulungu anamutenga Khristu, Mzimu; Mulungu Yehova anamutenga Khristu, pa mtanda, ndipo Iye anamung'amba Iye pakati. Iye anang'amba solo Yake ndipo anakaiyika iyo Mmwamba, ndipo anatenga thupi ndi kuliyika ilo mmanda. Ndipo analikweza mmwamba thupilo, mmawa wa chiwukitsiro; ndipo anatumizanso Mzimu umene unali pa Iye, kuti udzakhale pa Mpingo. Potero, chitsimikiziro chomwecho mmasiku otsiriza ano, "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," chimene pangano lomwelo linkayenera lidzakhale mwa anthu.

104 Inu mungawupeze bwanji Iwo kudzera mmaphunziro? Inu mungawupeze bwanji Iwo mwanjira iliyonse kupatula chitsimikiziro cha wamoyo, Yesu Khristu wowukitsidwa amene anawukitsidwa kuchokera kwa akufa ndipo akukhala mu Ukulu Mmwamba, usikuuno? Ndi Mzimu womwewo umene unali pa Iye, uli pa Mbewu Yachifumu ya Abrahamu, mmasiku otsiriza, kuvomerezera ndi kutsimikizira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ameni. Zimenezo zimakupangitsa iwe kumverera mwachipembedzo, sichoncho inu? Ndi zimenezotu, mu pangano lenilenilo, "Ndidzalemba pangano Langa pa mitima yawo." Yesu anati, "Zinthu zimene Ine ndikuchita inunso mudzazichita."

105 Pamene ife tikubwera apa ku Sodomu, mu maminiti pang'ono, penyani momwe izo zimakhalira, momwe izo zimachitikira kumeneko, ndendende momwe lonjezo liriri la tsiku lotsiriza ndi zomwe Iye akanadzachita.

106 Iye anali akutsimikizira izo, kusonyezera kuti Iye... Ine anang'amba thupi la Yesu pakati, anatenga Mzimu, anakweza thupilo ku dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Mulungu; ndipo anatsitsira pansi gawo linalo, gawo limene Iye analing'amba, Mzimu pa ife, umene umatchedwa Mzimu Woyera. Ndipo Moyo womwewo umene unali mwa Khristu uli mwa inu, zimenezo zimasonyeza kuti Iye ndi Muwomboli wanu. Iye anakukhazikitsani inu kukhala ana mwa Mulungu, ndipo tsopano ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ndi Mzimu wa Khristu. Ameni.

107 "Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita. Zazikulu kuposa izi inu mudzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga." Ameni.

108 Mzimu umene unali mwa Iye uli pa inu, Moyo Wamuyaya. Iye ndi wopereka wa Moyo Wamuyaya. Iye ndi Muwomboli, kuti adzabweretsenso icho chimene chinagwa mu kugwa, mu mtundu wa anthu, kuti adzabweretsenso kwa Mulungu. Ndipo Mzimu umene unali mwa Khristu uli mwa inu. Ndipo ngati mzimu wa a—a Dillon ukanakhala mwa ine, ine ndikanakhala ndi mfuti. Ngati mzimu wa wojambula ukanakhala mwa ine, ine bwenzi ndikujambula zithunzi. Ngati Mzimu wa Khristu uli mwa inu, ntchito za Khristu inu mudzazichita. Ameni. Uko nkulondola. Moyo umene unali mwa Iye uli mwa inu.

109 Mudzasamutse moyo kuchokera ku chirichonse kupita ku chinthu china. Ngati mungatenge moyo wa—wa dzungu ndi kuwuyika iwo mu mpesa wa mavwende, iwo ukhoza kubala maungu, chimodzimodzi. Inu mukatenga moyo kuchokera mu mtengo wa pichesi, ndi kuwuyika iwo mu mtengo wa peyala, iwo udzabala mapichesi, chifukwa moyo umene uli mu mtengo umapereka umboni wa izo.

110 Ndipo apo ndi momwe Mbewu Yachifumu; kudzera mwa Isaki panadzabwera mbewu yachibadwa, imene inayikana Iyo. Pa mtanda, kuchokera kwa Efraimu kupita kwa Manase, iwo anasamutsidwa, mdalitso kuchokera ku dzanja lamanja kupita ku lamanzere; kapena dzanja lamanzere linali la kumanzere, wamng'ono kwa wamkulu; kudzera pamenepo anatembenuza chochitika chonsecho kuchoka ku mbewu yachibadwa ya Isaki, imene inamukana Khristu, ndi mpingo wachibadwa lero umene ukumukanabe Iye.

111 Koma yauzimu, Mbewu Yachifumu ya Mulungu imene imakhulupirira, Mbewu Yachifumu ya Abrahamu imene imakhulupirira Mawu aliwonse a Mulungu, muli chitsimikiziro cha Yesu Kristu wamoyo, wowukitsidwa kwa akufa mwa iwo. Ameni. Ameni. Oh, mai! Mwaona, chinthu chomwecho chimene icho chinali, Mpingo wonse uyenera kukhala chibale.

112 Pamene izo zinaimiridwa mu mbewu yachibadwa, taonani, Isaki ndi Rebeka anali asuwani oyamba, chibale chamagazi, abambo omwewo; mwaona, abambowo anali abale, zinawapanga iwo kukhala asuweni amagazi, mkwatibwi ndi mkwati.

113 Ndipo mwa Adamu ndi Eva, izo zonse zinali Adamu, pa kuyamba pomwe. Mulungu anatenga nthiti kuchokera ku mbali yake ndipo anampanga mkazi, ndipo Iye anatenga mzimu wachikazi mwa Adamu ndipo anawuyika iwo mwa mkazi.

114 Chotero pamene mkazi achita zachimuna, pali china . . . pali kupotozedwa pamenepo penapake. Ndipo pamene mwamuna akufuna kukhala wachikazi wamkulu, pali chinachake cholakwika penapake. Mulungu anamupanga mwamuna ndipo anamuveka iye ngati mwamuna, ndipo mkazi ngati mkazi. Iye amafunabe iwo azikhala mwanjira imeneyo. Ameni. Pamene inu muwawona iwo akuchita chinachakenso, pali chinachake cholakwika. Icho chapotozedwa. Ndipo chinthu chonsecho chasanduka gulu la zopotoza. Ndiko kulondola ndendende. Mtundu wonse, m'badwo wonse, ndi, "chinthu chonsecho ndi chilonda chovunda," monga Baibulo linanenera. Palibe nkomwe kumveka paliponse. Inu mukudziwa izo ndi zoona. Inu simungampeze nkomwe—aliyense pakati pawo kumeneko . . . Koma kutuluka mu msewu, ndi zovuta kukapeza mwamuna weniweni; achikazi monga ine ndinayamba ndawawonapo. Ndipo akazi, iwo amavala matharauza, amameta tsitsi lawo, amapaka milomo, amasuta ndudu, kuyesetsa kuti akhale mwamuna. Kodi iwe ukufuna kukhala mwamuna za chiyani? Iwe ukuyenera kukhala dona.

115 Ine ndinawona chikwangwani, chinati, "Matebulo a madona," mchipinda chomwera mowa.

116 Ine ndinati, "Inu simunakhalepo ndi kasitomala." Dona sangapite ku malo oterowo. Ayi, bwana. Ayi, dona sangatero.

Mkazi akhoza, koma osati dona. Iye sangapite kumalo oterowo. Koma ndi inu pamenepo, mwaona.

117 Mulungu analekanitsa, anadula. Mwaona, Thupi, Mkwatibwi wa Khristu, ayenera kubwera kubwereraranso kwa woyamba. Tsopano Eva anali . . .

118 Kodi Eva anali chiyani? Iye ndi Adamu anali ofanana. Iwo ankatchedwa Adamu. Iwo anali mzimu. Pamene Iye anamupanga munthu, nthawi yoyamba, Iye anamupanga iye mu chifanizo Chake Chomwe. Ndipo Mulungu ndi Mzimu. "Mu chifanizo cha Mulungu anamulenga Iye iye, mwamuna ndi mkazi anawalenga Iye iwo." Iye anali . . . ndiyeno komabe apo panalibe munthu woti azilima mnthaka. Zitatero Mulungu anampanga munthu kuchokera mu fumbi la dziko lapansi ndipo anaika mzimu wapawiri uwu mwa iye, ndipo ameneyo anali Adamu woyamba.

119 Ndiye pamene Iye anamulekanitsa Eva kwa Adamu, Eva anagwa pa kusakhulupirira Mawu. Uko nkulondola. Ndi pamene mpingo walepherera lero, kusakhulupirira Mawu!

120 Koma mu nkhani iyi, kwa Mbewu Yachifumu, yoitanidwa, yokonzedweratu ku Moyo Wamuyaya, Mbewu Yachifumu ya Abrahamu, iwo amakhulupirira Mawu amenewo. Ine sindikusamala chimene chimabwera kapena kupita, kuchuluka kwa momwe iwo amasekera, yemwe amanena *izi*, *izo*, kapena *zinazo*, iwo anadzozedweratu ku Moyo Wamuyaya. Ndipo akupita molunjika kubwerera mmbuyo. Iye ndi Wokondedwa wake, Khristu, ndi ameneyo. Moyo, Mzimu umene uli mwa Khristu, uli mu Mpingo. Ndiro pangano lawo Lamuyaya, apa. Mukuona? Mulungu anatenga Mzimu wa Khristu, anawung'amba iwo pakati, pa nsembe ya pa Kalvare; ndipo anawutenga Mzimu umenewo, anakwezera mmwamba thupilo ndipo anakaliyika ilo pa dzanja lamanja la Mpandowachifumu wa Mulungu ndi Ukulu Mmwamba. Ndizo, chirichonse Kumwamba chikulamuliridwa ndi Iye. Ndiyeno Mzimu umene unali pa Iye, unadzabwerera; Mzimu womwewo, osati Mzimu wina, Mzimu womwewo unadzabwerera pa Iye, kudzatsimikizira pangano kwa Mbewu Yachifumu.

121 Ndipo mmasiku otsiriza ife tikuyenera kuziwona izo, molingana ndi Lemba. Ndipo Mkwatibwi wa Khristu asanatengedwere mmwamba, payenera kukhala pali utumiki wolumikizana chimodzimodzi. Ameni. Ndine wokondwa kunena, usikuuno, kuti ine ndikudziwa kuti ndicho Choonadi. Ameni. Kulumikizana, kutsimikizira pangano!

122 Iye anatsimikizira izo pamenepo, anamusonyeza iye chimene Iye akanati adzachite, kutsimikizira pangano. Sikolala aliyense wa Baibulo amadziwa kuti ndi pamene Iye anatsimikizira pangano kwa Abrahamu. Kodi Iye anali kuchita chiyani?

Kuwonetsa mu chifaniziro, chimene Iye akanati adzachite, ndi nsembe izi.

123 Ndipo tsopano kwayamba kuda, ndipo ine sindikhala ndi nthawi yogawa nsembe izi. Ine ndiyenera kuti mwina ndidzachite zimenezo mawa usiku, koma, zindikirani, kusonyeza chimene iwo, chimene nsembe izi zinkatanthauza. Koma, onani, Iye anatsimikizira izo, kusonyeza kuti mmasiku otsiriza . . .

124 Tsopano aliyense amene anayamba wawerengapo mbiri yakale, amadziwa kuti umo ndi momwe iwo ankapangira pangano. Iwo ankalemba izo, kenako ankang'amba izo, ndipo ankapereka; mmodzi ankatenga chidutswa chimodzi, ndipo winayo chinacho. Iwo ankayenera kuti abwerere, pa nsembeyo, kudzapereka nsembe yawo. Ndicho chimene Abrahamu anachita kwa . . . uko ku Gerari, ndi zina zotero, kumene iye anapita kumeneko, kumene iwo anakapereka guwa . . . anakapereka nsembe yawo ndipo anapanga migwirizano yawo, ndi kuzing'amba izo pakati monga choncho. Ndipo Mulungu anachita chinthu chomwecho, kusonyezera pamenepo kuti chimene Iye akanati adzachite kwa A- . . .

125 Funso linali lakuti, "Ili kuti—ili kuti Mbewu iyi yomwe inu munandilonjeza ine? Kuti? Ine ndikhala motani imeneyo? Anthu akundiseka ine, akumati, 'Abrahamu, atate wa mafuko, wakhala zaka fifitini. Tsopano inu muli ndi zaka eyite-faivi zakubadwa, kapena—kapena nainte. Kuti, kuti, kuti, ali kuti ana ako onsewo? Kodi uli ndi ana angati tsopano, atate wa mafuko?'" Mwaona, kumuseka iye. Koma iye sanadzandime ayi. Iye anakhala nachobe icho. Kusekedwa, ankati, "Atate wa mafuko, tsopano tiyeni tiwone, kodi inu muli ndi ana angati pa nthawi ino?" Mwaona, kufuna kumuseleula, chifukwa iye anali akugwira ku malonjezo a Mulungu, akukhulupirira kuti Iye ndi wokhoza kusunga chimene Iye analonjeza. Iye ali—Iye ndi wokhoza moposa. Iye ali . . .

126 Iye akhoza kupereka nsembe Yake Yomwe. Iye ndi Yehova-Yire. Iye akhoza kupereka ndi kukonza njira ya chimene Iye analonjeza. Ndipo Iye anatsimikizira panganolo kwa iye pomuwonetsa iye momwe Iye akanati adzachitire izo, pakumutenga Khristu ndi kung'amba Moyo kuchokera kwa Iye, ndi kuwutumiza iwo pansi mmasiku otsiriza . . .

127 Tsopano ife titsiriza zimenezo mu Lemba, sabata ino, kuti titsimikizire izo kwa inu, kuti pangano ili liyenera kutsimikiziridwa ndi Mbewu Yachifumu ya Abrahamu, amene ali anthu ochokera mwa Amitundu, osati Ayuda, "anthu ochokera mwa Amitundu, chifukwa cha Dzina Lake," kuwatenga iwo chifukwa cha Dzina Lake. Mpingo umene uli ndi Dzina Lake udzabwerera mwa Iye, chifukwa ndi yemwe Iye ali, Moyo wake.

128 Mvetserani, pamene pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mzimu Woyera unagwa pa Tsiku la Pentekoste, Moyo unaperekedwa kwa Mpingo. Ndipo Mpingo uwo umene unapita kumeneko ndi kukabala, iwo analemba kuseri kwa Mpingo umenewo Bukhu la Machitidwe, za zomwe Iwo unachita, chifukwa iye anali Khristu mwa atumwi.

129 Tsopano Yesu anati, mu Yohane Woyera 15, "Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi zake." Tsopano, Mpesa sumabala chipatso. Nthambi zimabala zipatso. Izo zimapatsidwa mphamvu ndi Mpesa. Chabwino, tsopano, ngati nthambi imeneyo, yoyamba kutulukira pa mtengo umenewo, inabala Bukhu la Machitidwe; ngati iyo iti idzatulutse konse nthambi ina, iwo udzakhala Moyo womwewo.

130 Miyezi ingapo yapitayo, ine ndinali kuyima ndi mzanga wabwino, John Sharrit, uko ku Phoenix. Ine ndimakhala ku Tucson, monga inu mukudziwira. Ndipo kotero ine ndinali ku Phoenix, M'bale John Sharrit, m'bale wabwino kwambiri wa Chikhristu. Ndipo iye anali weniweni, wosauka kwenikweni, ndipo Ambuye amudalitsa iye. Ndipo—ndipo pamene ine ndinapita koyamba ku Phoenix, zaka zapitazo, iye analibe ana. Ndipo—ndipo iye anali kufuna ana. Ndipo—ndipo iwo, wosauka, akugwira ntchito pa msewu, akuphulitsa konkire, pafupifupi twente-faivi, ma senti sarte pa ora. Ndipo iye anabwera kumusi uko, ndipo iye anakhulupirira Mawu aliwonse a Uthenga. Ndipo iye anati, "Kodi inu mungandipempherere ine?" Iye ali ndi ana faivi tsopano.

131 Ndipo zimenezo, pambali pa zimenezo, iye amapereka pafupifupi madola mamillioni atatu mpaka foro chaka chirichonse ku ntchito ya Khristu. Ndipo ndiko kulondola. Ine ndinali naye kuno, osati kale kwambiri, amayendera munda wake wa thonje. Iye anagula chigawo chonsecho, anali ndi anthu aku Mexico fifitini handiredi amene amasamalira zimenezo. Ndipo zinali, zaka fifitini zapitazo anali akuphulitsa konkire, kumalandira masenti twente-faivi pa ora.

132 Iye ananditengera ine uko m'munda wake waukulu wa zipatso za citrus. Ndipo ine ndinawona mtengo wowoneka moseketsa, mmenemo, umene ine ndinayamba ndawuwonapo mmoyo wanga. Iwo unali mtundu wina wa mtengo, iwo unali ndi mitundu yonse ya zipatso pa iwo. Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo iwo unali ndi malalanje, iwo unali ndi mandimu, iwo unali ndi zipatso za manyumwa, iwo unali ndi mananchesi, unali ndi tangelo. Ine ndikuganiza kuti panali mitundu naini ya zipatso, kapena teni. Ndipo ine ndinati, "Ndi mtundu wanji wa mtengo umenewo?"

133 "Oh," iye anati, "uko ndikuyeserera pang'ono chabe, M'bale Branham."

134 Ine ndinati, "Oh, chabwino." Ndipo ine ndinati, "Izo zonse zikukhala pa mtengo umodzi umenewo?" Ine ndinati, "Ndi mtengo wa mtundu wanji umenewo, kuyamba ndi kuyamba?"

135 Iye anati, "Ndi mtengo walalanje. Ndi lalanje la mchombo."

136 Ndipo ine ndinati, "Ilo liri?" Ine ndinati, "Nanga zinazo zikuchita chiyani pamenepo?"

Ndipo iye anati, "Izo zinamezanitsidwa mwa iwo."

137 Ine ndinati, "Oh, chabwino." Ine ndinati, "Ine ndikumvetsa." Ine ndinati, "Tsopano, tsopano chaka chamawa, chirichonse chidzabwerera kudzakhala lalanje, sichoncho izo?"

138 Anati, "Oh, ayi." Anati, "Ayi, mandimu adzabala mandimu." Iye anati, "A. . .ndipo manyumwa adzabereka zipatso za manyumwa, ndipo nanchesi adzabereka mananchesi."

Ine ndinati, "Kuchokera mu mtengo walalanje?"

Iye anati, "Inde, bwana."

Ine ndinati, "Ine sindikuwona momwe izo zingachitire zimenezo."

Anati, "Izo zonse ndi zipatso za citrus."

Ine ndinati, "Chabwino, Ambuye alemekezeke! Ine ndikuwona chinachake."

139 Taonani! Oh, m'bale, pamene Mzimu Woyera umenewo unabwera mu Mpesa umenewo, ndi kudzabala kuchokera mu Mpesa wake kupita ku nthambi yoyamba, ndipo iwo analemba Bukhu la Machitidwe kumbuyo kwake, ngati mtengo umenewo uti udzatulutse konse nthambi yapachiyambi, iwo udzamera chinthu chomwecho. Icho chidzakhala Yesu Khristu. Tsopano ife tiri nawo Amethodisti, Apresbateria, Abaptisti, Achilutera, china chirichonse chamezanitsidwa mwa iwo, kumabala chipatso cha chipembedzo; koma ngati iwo udzabale konse nthambi ina, iwo udzakhala weniweni, wodzazidwa-Khristu, Mawu a Mulungu okhazikika pa Khristu.

140 Ndipo, kumbukirani, inu mukukumbukira uthenga wa *Mtengo Wa Mkwatibwi*. Ambiri a inu mumatenga tepi. Momwe kuti wosamalirayo anatulukira, ndipo iwo unali kubala mtundu wa chipatso chosayenera, kotero iye anadzaidula iyo, anaidula iyo, akupitiriza kuidulanso iyo, kuidulanso iyo. Koma Yoweli anati, "Chimene chimbalanga chinasiya, anoni anachidya; chimene chimba-. . .anoni anasiya, chinachakenso chinadya." Ife tikupeza kuti tizirombo timeneto ndi tizirombo tomweto, kokha mmasiteji osiyanasiyana. Ndipo chimene Achilutera anasiya, Amethodisti anadya; chimene Amethodisti anasiya, Abaptisti anadya; chimene Abaptisti anasiya, Achipentekoste anadya. Chinthu chonsecho chadulidwa.

141 Koma Mulungu anati, "Ine ndidzabwezeretsa, atero Ambuye, zaka zonse. Ine ndidzatumizanso Mpingo

wina, mmasiku otsiriza. Ine ndidzabwezeretsa Mphamvu yapachiyambi ija kachiwiri. Ine. . . Mu nthawi ya kumadzulo, kudzakhala Kuwala." Pansi mu mtima wa mtengo umenewo, ziribe kanthu kuti ndi nthambi zingati zomwe zidulidwapo, pamenepo padzatulukira Mbewu Yachifumu ya Abrahamu! Aleluya! Mulungu analonjeza zimenezo. Mulungu adzachita izo. Iye anati Iye akanadzachita izo. "Ine ndidzabwezeretsa zaka zonse zimene zipembedzo zinadya. Ine ndidzabwezeretsa zaka zonse. Ine ndachidulira chinthucho, komabe padzabwera Mpesa kuchokera mu mtima wa iwo. Iye adzakhala ngati mtengo wobzalidwa m'mphepete mwa mitsinje ya madzi, munthu yemwe amasinkhasinkha mu Mawu a Mulungu, usana ndi usiku," osati ku kachikhulupiriro kapena chipembedzo, "koma amasinkhasinkha mu Mawu, usana ndi usiku. Iye adzakhala ngati mtengo umene wabzalidwa m'mphepete mwa mtsinje wa madzi; nthambi sizidzafota ayi. Iye adzabala zipatso zake mu nyengo yake." Mulungu analonjeza zimenezo.

142 Mulungu, akudzing'amba, akudzisololamo, akudziganga, akudzilekanitsa Yekha, akudzigawa Yekha. Iye anachita chinthu chomwecho pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mzimu Woyera unadzatsika. Lawi la Moto lija linatsika, lomwe linkatsatira Israeli, ife tonse tikudziwa kuti iyo inali Logos, ameneyo anali Khristu. Ndipo pamene Iwo unatsika, pa Tsiku la Pentekoste, kodi Iwo unachita chiyani? Iwo unadzigawa Wokha, ndipo malirime a Moto anadzakhala pa aliyense wa iwo. Mulungu akudzigawa Yekha pakati pa anthu. Oh, m'bale, inu mukhoza kukhala osagawanika, ndi Mzimu womwewo umene unali mwa Khristu.

143 "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita. Zazikulu kuposa izi, kapena *zochuluka* kuposa izi," kumasulira koyenera "pakuti Ine ndikupita kwa Atate. Komabe, kanthawi pang'ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine," puronauni ya umwini, "Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, pa nthawi yotsiriza, chimaliziro." Iye analonjeza kuti adzachita zimenezo. Mbewu ya Abrahamu, Iye ali pano tsopano. Iye ndi . . .

144 Ife tiri pano, masiku angapo apitawo, tikukondwerera chiukitsiro cha Iye, kuti Mulungu anamuukitsa Iye. Ife timachitira umboni zimenezo. Ife timayimba zimenezo. Ndipo Iye akhoza kuwonekera ndi kuchita chinachake chimene Iye anachita, monga momwe Iye anachitira chisanachitike chiwukitsiro Chake, ife tikhoza kuzitcha izo, "wambwebwe, mdierekezi, Belezebule," kuzitsekera izo kunja kwa mpingo. Kodi ife timachitiranji zimenezo? Ayenera kukwaniritsa Lemba, kuti, mu M'badwo wa Laodikaya, Mawu, amene anali Khristu, anali ataikidwa panja, [M'bale Branham akugogoda pa guwa—Mkonzi]. akugogoda pa chitseko, kuyesetsa kuti

apeze mgwirizano wina kuchokera kwinakwake, adzalowe ndi kudzadziziwitsa Yekha.

145 Koma padzabwera nthambi kuchokera Kumeneko, motsimikiza basi monga chirichonse!

146 Ine ndinati kwa M'bale Sharrit, "Ndiye ndi nthambi ya mtundu wanji yomwe iwo udzabale chaka chamawa? Kodi iyo idzakhala lalanje? Kodi iyo idzakhala mandimu? Idza . . . "

147 "Inde, iyo idzakhala yapachiyambi," iye anatero. "Pamene iwo udzabale nthambi kuchokera mwa iwowo, iyo idzakhala ya lalanje, monga izo zinali pachiyambi."

148 Ndipo pamene Mbewu yeniyeni, yamoyo ya Abrahamu inabwera, Mzimu womwewo umene unali mwa Yesu Khristu udzakhala pakati pawo, Mawu aliwonse adzavomerezedwa ndi "Ameni." Iwo adzawakhulupirira Iwo. Osati, "*Izi* ndi zowuziridwa, ndipo *Izo* si zowuziridwa." Iwo amakhulupirira Chinthu chonsecho, chifukwa Icho ndi Mawu a Mulungu.

149 Kodi inu mukukhulupirira Iwo, usikuuno, ndi mtima wanu wonse? Ine ndikukhulupirira zimenezo.

150 Ine ndalalikira kale apa tsopano mpaka zatenga nthawi yaitali. Tiyeni tiweramitse mitu yathu miniti yokha. Ndipo ine ndidzatsirizitsa izi mawa usiku. Ine ndinalonjeza kuti sindikusungani mochedwa.

151 Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwa . . . Zinatsimikiziridwa, izo zinakhazikika ndi Abrahamu, pamene mwa chikhulupiriro iye anaziwona izo, anapitabe chitsogolo, osazandima mu kusakhulupirira. Iye sanazandime ayi. Tsopano nanga bwanji Mbewu Yake Yachifumu, ife amene timadzinenera, ife Akhristu a tsiku lino, amene amadzinerera kuti amapysopsyona chikho chomwecho chimene Iye anamweramo, kukhala nawo Mzimu Wake womwewo mkati mwathu, ndi kumuwona Iye akutsimikizira lonjezo Lake la kukhala pano ndi ife?

152 Lonjezo, kulipanga ilo kukwaniritsa, sizinayambe zakhala chomwecho mmibadwo yonse. Ife sitinayambe takhalapo nazo izo kale. Fufuzani mbiriyakale. Izo sizinayambe zawonekerapo konse. Ndipo kodi Iwo unkayenera kupita kuti mmasiku otsiriza? Kwa Mpingo wosankhidwa. Osati ku Babeloni, osati kwa Sodomu; iwo anali naye mtumiki kumusi uko. Koma Mzimu Woyera ndi Mtumiki kwa Mpingo wosankhidwa, usikuuno, Mulungu akukhala mu thupi la munthu, akudziwonetsera Yekha, Wozindikira, Mawu amene amazindikira malingaliro ndi zamkati mwa mtima. "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Iye ndi Yehova-Yire. Iye wapereka kale Nsembe yathu, ndipo akutsimikizira pangano Lake. Iye akusunga pangano Lake, mmasiku otsiriza, ndi anthu.

153 Abwenzi, ife tikhoza kuyankhula pano usiku wonse. Zinthu zimene zanenedwa, pali zokwanira zomwe zanenedwa. Pali anthu pano amene akudwala; inu mukusowa machiritso. Bwanji osakhulupirira Iwo? Ngati ine ndikanakhoza kukuchiritsani inu, ine ndikanachita zimenezo. Khalani mukupemphera. Ngati ine ndikanakhoza kukuchiritsani inu, ine ndikanachita izo. Ine sindingakhoze kukuchiritsani inu. Ndine . . . Inu mukuzindikira, ine ndipereka msonkhano, usiku woyamba kapena wachiwiri, pano, pa kupempherera odwala. Ndipo si za izo zokha. Ngati pali Mbewu iliyonse pano yomwe inadzozedweratu ku Moyo, Mzimu Woyera uyigwira iyo. Iwo aziwona izo. Iwo azidziwa izo. Tsopano Iye ali . . .

154 Ndi angati muno amene angakweze manja anu, pamaso pa Mulungu, ndi kuti, "Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse, kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; kuti Iye anauka kwa akufa, ndipo Iye ali wamoyo pakati pathu usikuuno, akudziwonetsera Yekha kuti ali pakati pathu, ndipo ine ndikukhulupirira kuti izo ndi za Mulungu"? Kodi inu mungakweze manja anu, ndikuti, "Ine ndikukhulupirira izo moona"?

155 Tsopano, Atate Akumwamba, iwo ali mmanja Mwanu. Iwo ali . . . Iwo akudzinenera kuti iwo ndi Mbewu ya Abrahamu. Iwo—iwo akufuna, iwo—iwo akufuna madalitso a Mulungu. Ndipo tsopano ine ndawauza iwo, mwa njira yophweka iyi, yaing'ono. Ine ndinayamba pa mutu wanga, ndipo sindinafike pomaliza iwo. Koma, Atate, iwo—iwo akuwona apa, mu kutsimikizira kwa Abrahamu, kuti Inu munatsimikizira lonjezo kwa iye, mumamupatsa iye chitsimikiziro. Tsopano ngati a—ngati Mzimu wa Khristu suli mwa ife, ndiye ife sitiri kanthu ka Khristu. Ndipo chikhalidwe cha Khristu sichingakhoze kusinthidwa.

156 Ndipo Iye anatiuza ife bwino, ndipo walonjeza zinthu izi molingana ndi Baibulo, mmalo ambiri. Ngakhale Chipangano Chakale chinalonjeza zimenezo, mu Malaki 4, momwe izo zikanati zidzakhalire mmasiku otsiriza, "Adzatembenuzira mitima ya ana kubwerera ku Chikhulupiriro cha makolo," monga atate Achipentekoste, Chiphunzitso chapachiyambi cha Baibulo, Mawu apachiyambi, chimene Iwo akanati adzachite. Ndipo padzakhala chizindikiro, ndipo chizindikiro ichi chikanadzatsimikizira, kutsimikiziridwa ndi Liwu limene likanati lidzatsatire icho, kuti Inu muli pano. Ndipo ife tikukukhulupirirani Inu.

157 Tsopano, Atate, mulole—mulole Satana apange njira yake yotulukira. Ife—ife sitikhulupirira kuti tiri nayo mphamvu iliyonse, Ambuye. Ife sitikudzinenera kuti tiri nayo mphamvu. Ife timadzinenera kuti tiri nawo ulamuliro.

158 Ife timazindikira, wapolisi wamng'ono pa msewu, ali ndi

chipewa chaching'ono chitakhala pamutu pake, magalimoto akuluakulu akusesa kudutsa mmisewu imeneyo, mailosi nainte pa ora, ndi injini ya mphamvu za akavalo firii handiredi, iye alibe mphamvu yoimitsira imodzi ya iwo. Iwo akhoza kungomuphwanyira iye pansi. Koma mungomulola iye awonetse baji imeneyo, ndi kukweza manja ake, mabuleki azilira ndipo matayala azing'ung'uza. Ndi ulamuliro. Mzinda wonsewo uli kumbuyo kwake. Iye ali nawo ulamuliro, osati mphamvu. Iye akhoza kusalemera mapaundi handiredi, koma iye ali nawo ulamuliro.

159 Ndipo umo ndi momwe izo ziriri usikuuno, Ambuye. Ife tikubwera kwa Satana, osati ndi mphamvu, koma ndi ulamuliro, kusonyeza Magazi ndi kutsimikizira kwa pangano. Iye alibe ufulu wowagwira anthu odwala awa.

160 Kuyang'ana pa iwo ndi kuwawona iwo akutuluka nazo thukuta, apa, O Mulungu, ngati pali njira ina yomwe ine ndingakhoze kungotengera Uthenga kwa iwo! Ngati iwo atangokhoza kupenya, Ambuye, kungozindikira chabe! Adzutseni iwo, Ambuye. Nthawi imodzi tsopano, usikuuno, aloleni iwo awone kuti Ndinu Mulungu yemweyo. Inu mukutsimikizira Mawu Anu. Inu muwasunge Iwo basi monga Inu munalonjezera. Mmasiku otsiriza ano, Inu munati zinthu izi zidzachitika, "Pamene Mwana wa munthu azidzawululidwa," kuti zinthu izi zikanadzachitika. Perekani izi, Ambuye, ndipo aloleni iwo awone kuti ndi Inuyo. Mu Dzina la Yesu, ine ndikupemphera. Ameni.

161 Tsopano khulupirirani, abwenzi. Ndinu omvetsera abwino kwambiri. Ine ndangodutsitsa nthawi yanga, mwaona, ndipo ine—ine sindimatanthauza kuti ndichite zimenezo. Ine ndinawauza iwo ine. . . ife tituluka mu nthawi yake, usikuuno, koma ine ndalephera chifukwa ine. . . Ndipo ine ndidzatsiriza mutu wanga mawa usiku, mwinamwake, Ambuye akalola.

162 Tsopano ife tiri pano. Anthu anu. Ndife tonse anthu okhalapo basi. Ife tikufuna kukhala ndi moyo. Aliyense amafuna kukhala nthawi yake. Ine ndikukhulupirira Mulungu akufuna kuti ife tichite zimenezo. Ine—ine ndikukhulupirira zimenezo. Tsopano, si chifukwa chakuti kulibeko Mvunguti ku Giliadi.

163 Inu mukudziwa, izo zinanenedwa nthawi ina, "Chifukwa chiyani, chifukwa chiyani ziri chomwecho? Kodi—kodi kulibeko mvunguti ku Giliadi?"

164 "Kodi kulibeko mneneri kumeneko?" Yesaya anatero, kapena, ine ndikutanthauza Eliya anatero. "Pitani mukamufunse iye, 'Kodi ndi chifukwa chakuti mu Israeli mulibemo mneneri? Ndi chifukwa chiyani inu mukupita ku Ekroni kumtunda uko, mulungu Baala-zebubu? Bwanji, chiyani, inu mukupita kumeneko?' Iye pokhala Myuda, 'Bwanji inu mukumapita uko?'"

165 Anati, "Kodi ndi chifukwa chakuti ku Giliadi kulibeko mvunguti, kulibeko sing'anga kumeneko? Kodi alipo? Kodi ndicho chifukwa chake?"

166 Chifukwa chake ndi chimenecho? Ayi, Bwana. Ife tiri ndi Mvunguti. Mzimu Woyera uli pano. Inde, bwana. Lonjezolo ndi lathu. Tsopano inu muyenera kungokhulupirira izi. Inu . . .

167 Ndi tsiku lomwe malingaliro a anthu amwazikana kwambiri, iwo sakutero . . . Ine ndikuwamvera chisoni iwo. Iwo sakudziwa choti akhulupirire. Wina akunena *izi*, ndipo wina akunena *izo*. "Ndipo mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale owona," Ambuye Mulungu anati. Ndiko kulondola. Tsopano Iye sangakhoze kusintha chikhalidwe Chake.

168 Tsopano, ine ndikukhulupirira usiku wathawu ife tinayambitsa khadi la pemphero loyamba (sichoncho izo?), ndipo tinaitana mpaka pafupifupi twente, kapena chinachake chonga icho. Huh? Tiyeni tisinthe ndondomeko imeneyo. Tiyeni tisakhale ndi makadi apemphero aliwonse. Inde, inu muzingopemphera. Inu mukudziwa, khadi la pemphero limangokufikitsani inu kuno.

169 Koma ine ndikumverera Kukhalapo Kwake, kotero ine ndikungodziwa Iye ali pano. Ndi angati anayamba anawonapo chithunzi cha Mngelo wa Ambuye uja? Kotero ndithandizeni ine, pamene ine ndidzakomane nanu pa Chiweruzo, Iye siali mapazi awiri kuchokera pamene ine ndaimapa pomwe apa. Izo nzoona. Ali pano.

170 Tsopano winawake yemwe alibe makadi apemphero, kwezani mmwamba dzanja lanu, ndikuti, "Ine ndiribe makadi apemphero, ndipo komabe ndikudwala ndi wosowa." Chabwino, iwo ali paliponsepo. Chabwino.

171 Tsopano ine ndikukuuzani inu. Kodi Mngelo uja anachita chiyani kumeneko nthawi imeneyo? Iye anatembenuza nsana Wake, anali atatembenuzira nsana Wake kwa Abrahamu. Chimene, ine ndimati ndifikeko, usikuuno, ndipo sindinachite zimenezo. Ndipo pamene Iye anati, "Icho chikanadzakhala chinthu chomwecho pa Kudza kwa Ambuye, monga izo zinakhalira ku Sodomu." Ife tikupeza kuti, Iye anali atatembenuzira nsana Wake ku hema. Ndipo Sarah anaseka pa zomwe Iye ananena, chifukwa Iye anamuuza iye. Ndipo iye sanakhoze kumvetsa zimenezo, pongokhala Munthu kunja uko, akudya nyama yomwe iye anakazinga, kumwa mkaka wa ng'ombe, ndi kudya ng'ombe yake, ndipo ameneyo anali Mulungu.

172 Baibulo linati iye anali. Abrahamu anati iye anali, "Elohim." Uko nkulondola. "Elohim," *Mulungu*. Iye anazimirira Abrahamu akuyang'ana. Ndipo, "Mulungu," anamutcha Iye, "Ambuye Mulungu, Elohim, Wokwanira mu Zonse."

173 “Pachiyambi,” mawu omwewo amagwiritsidwa ntchito. Sikolala aliyense amadziwa zimenezo. “Pachiyambi *Mulungu*,” muyang’ane mu Ahebri, “Elohim.”

174 Penyani pamene Abrahamu anati, “Ambuye Mulungu, Elohim,” Mwamuna yemweyo, Munthu yemweyo, kusonyeza kuti Mulungu adzadziwonetsera Yekha mu thupi laumunthu, kwa Mbewu ya Abrahamu, kuti adzatsimikizire pangano, ndi kudzachita chinthu chomwecho chimene Iye anachita, (mukuona zimenezo?) chinthu chomwecho chimene Iye anachita kumeneko. Iye nthawizonse amakhala mneneri amene amazindikira malingaliro ndi zamkati mwa mtima. Chifukwa, ndi angati akudziwa kuti Baibulo linanena chomwecho, “Mawu a Mulungu amazindikira malingaliro amene ali mu mtima”?

175 Tsopano ngati Mulungu ati atenge osachepera anthu atatu muno, usikuuno. Tsopano ichi ndi chitsutso. Ngati aliyense sakuganiza kuti ziri chomwecho, inu mubwere mudzachite zimenezo. Ngati iwo sangatero, ndiye musati munene kanthu za izo. Mukuona? Tsopano, zindikirani, kutenga osachepera anthu atatu, (atatu ndi kutsimikizira), awo ndi alendo kwathunthu, ndipo ngati Mzimu Woyera. . . Ngati inu mungokhulupirira, ndizo zonse zomwe ine ndikukupemphani inu kuti mukhulupirire, kuti muchite, ndi kukhulupirira kuti Baibulo *ili* ndi Choonadi, ndipo ife tikukhala mmasiku otsiriza, ndipo ili ndi lonjezo la masiku otsiriza.

176 Kumbukirani, Abrahamu, kapena palibe wina aliyense, anawona chizindikiro china chirichonse mpaka Mwana wolonjezedwa atadzabwera powonekera. Abrahamu anawona mitundu yonse ya zizindikiro ndi zinthu, mpaka pamenepo, koma chimenecho chinali chizindikiro chotsiriza. Iye sadzaswa konse zimenezo; kupitirizika kwa Mulungu. Mbewu ya Abrahamu, ndicho chizindikiro chawo chotsiriza. Mukuona? Chimenecho chinali chotsiriza. Mulungu! Iye anadziwa, apo pomwe, ameneyo anali Elohim. Ndipo Yesu anapotoloka ndipo anati izo zikanadzakhala mwanjira imeneyo, ndipo apa ife tiri pomwe apa lero pa zimenezo, chinthu chomwecho.

177 Anthu, ichi ndi Choonadi. Ine ndikudziwa, “Pomwe pano mu barani yaing’ono?” inu munanena. Chabwino, izo nthawizonse zakhala ziri mwanjira imeneyo. Iye anabadwira modyera ng’ombe. Panalibe nkomwe aliyense akanamukhulupirira Iye. Koma ndi Mbewu zokhazo zomwe zimakhulupirira, zomwe zinakonzedweratu ku Moyo, ndizo zonse. “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine.” Uko nkulondola. Simukuyenera muzidandaula, kuti; dzina lawo liri pamenepo, iwo adzaliwona ilo. Ndipo motani? Iwo adzachita zimenezo.

178 Tsopano, onani, lingaliro lokha, ine—ine ndikhoza kupemphera ndi kuika manja pa inu. Ine ndidzayankhula pa zimenezo, makamaka Lamlungu madzulo. Koma ine—ine

ndikufuna inu muwone kuti inu mukhoza kusanjika manja anu pa Iye. "Iye ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu." Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Amene."—Mkonzi]. Inu mukukhulupirira izo. Ndipo tsopano ngati Iye ati achite izo . . .

179 Ine—ine ndikumudziwa winawake pano. Ine ndinapezeka ndikuyang'ana uko, ndipo ine ndinawona amzanga awiri kapena atatu atakhala pamenepo, ameneyo ndi mtumiki, angapo a iwo kumeneko. Ndipo wina waweramitsa mutu wake pansi, Ambuye amuchiritsa kumene mnyamata wake wamng'ono, kuchokera ku kugwedezeka kwa ubongo, komabe, lero, anandiyimbira ine telefoni.

180 Ndipo—ndipo mwamuna wina kumeneko, ndi mwana wake wamng'ono, usiku wina, iwo ankaganiza kuti iye wamwalira. Ndipo ine ndinali ku Beaumont. Ndipo ife, ataitana, ndinapitako, ndipo iye anadzaika manja ake pa ine, nkuyamba kulira, anati, "M'bale Branham, Mawu a Ambuye ali ndi inu. Ingomupemphani Iye." Pa miniti yomweyo, mwana wamng'onoyo anabwerera ku moyo, ndipo anakhalanso ndi moyo. Bambo ake ndi awo akhala pomwe apowo, mtumiki.

181 Ndipo bambo uyu, galimoto inachita ngozi, ndipo inamuponyera iye kudutsa mu chinachake kapena chimzake, ndipo kulumpha mpaka mdzenje, ndipo anasokoneza ubongo wake waung'ono, ndi zinthu. Ambuye anamuchiza iye, ali bwinobwino mwangwiro. Iwo anakhulupirira. Iwo mwamtheradi . . .

182 Tsopano musanene kuti ine ndinachita zimenezo. Ine ndinalibe chochita nazo izo. Chikhulupiriro chawo mwa Mulungu, ndi chimene chinachita izo. Inu mukhale ndi chikhulupiriro! Zonse . . .

183 Yesu ananena, mu Marko Woyera 11:22, "Chinthu chirichonse! Ngati mudzanena kwa phiri ili, 'Sunthidwa,' ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti zomwe inu mwanena zidzachitika, inu mukhoza kukhala nazo zomwe inu mwanenazo." Koma ndi zimenezo pamenepo, mwaona. Si chiyembekezo; ndizo "ndikudziwa izo."

184 Ndipo ngati Iye angakhoze kudzitsimikizira Yekha wamoyo, Mmodzi yemwe anapanga lonjezo akhoza kudzitsimikizira Yekha wamoyo, ndipo palibe china mdziko chingakhoze kuchita izo. Dzukani! Dzigwedezeni nokha, mwamphamvu kwenikweni, mzimu wanu. Mukuona? Palibe kanthu mdziko kangakhoze kuchita zimenezo koma Mulungu.

185 Tsopano inu mukhoza—inu mukhoza kuwuweruza iwo woipa, ngati inu mukufuna kutero. Iwo anamuweruza Iye woipa, kotero iwo akhozabe kuwuweruza Mzimu Wake woipa. Iwo

anati, “Iye anali mdierekezi, akuchita zimenezo.” Chabwino, ndithudi, iwo analandira mphotho imeneyo.

186 Inu mungokhulupirira. Inu simungakhoze kuchiritsa. Ine sindingakhoze kuchiritsa. Palibe munthu angakhoze kuchiza. Mulungu ndiye mchiritsi.

187 Koma ngati mungakhoze kungozindikira kuti Mmodzi yemweyo yemwe inu mumamutumikira, ndipo munadzilekanitsa nokha kwa dziko kuti mukamutumikire, Mmodzi yemweyo amene inu mumamukonda; Mmodzi yemweyo yemwe ati adzayime pa Chiweruzo, inu pa Chiweruzo ndi Iye, kuti mudzaweruzidwe, ngati Kukhalapo Kwake kutabwera pomwe pano ndi kudzasonyeza kuti Iye ali pano!

188 Tsopano thupi Lake logwirika silingakhoze kuchita zimenezo. Pamene ilo lidzafike, nthawi yatha. “Monga mphezi imachokera Kummawa kupita Kumadzulo, chomwechonso kudza kwa Mwana wa munthu.” Koma, Mzimu Wake!

189 Ndipo Mpingo wabwera, taonani momwe iwo watulukirira; kudzera mu kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera; ndipo tsopano mpaka mu nthawi yokwatulidwa, kuti awukonzekeretse Mpingo. Ndendende basi momwe izo zinalonjezedwera, basi momwe Mibadwo ya Mpingo inafoletsedwera, ndipo ife tinaziwona izo, chirichonse chikubwera chotsika, ndipo mpaka mmusi.

190 Pentekosite ndi bungwe lotsirizira. Ndizo molingana ndi Lemba. Ilo lidzakhala bungwe lotsirizira, lokanidwa ndi ena onsewo, ndiko kulondola, monga bungwe. Palibe bungwe lomwe limavomerezedwa kwa Mulungu. Ndi a . . . Ndi munthu payekha, ndi omwe amavomerezedwa kwa Mulungu.

191 Tsopano kodi inu simukukhulupirira Kukhalapo Kwake? Tsopano apa, ine ndangokhala m’bale wanu, ndipo tsopano ndinatumizidwa, kuti Mulungu anandiuza ine kuti ndibwere ndizidzachita izi. Chotero, ine ndikumukhulupirira Iye. Ndipo ngati izo zikanakhala kuti sizinalembedwe mu Mawu, a m’badwo uno, ine ndikanachokako kwa izo. Chirichonse chimene mulibemo mu Mawu amenewo, ine sindimazikhulupirira izo. Ine—ine sindingazivomereze izo. Ine sindikunena kuti sindingazikhulupirire izo, koma sindizivomereza izo; ine sindizimvetsa izo. Koma pamene izo ziri mu Mawu awa, komanso ndi lonjezo la m’badwo uno, ine ndikuzimvetsa izo. Si choncho inu? Ambuye atithandize ife tsopano. Ndipo inu basi . . . Inu mufikire kumeneko tsopano, mwa chikhulupiriro, mukhulupirire zimenezo mu . . . kukhalapo kwathu . . . Ife tiri mu Kukhalapo Kwake, kani, tsopano, ndi Yesu yemweyo amene anapanga lonjezo limenelo.

192 Ndipo mu Baibulo apa, Paulo wodzozedwayo, yemwe anali ndi mavumbulutso mochuluka chomwecho mpaka ankamupangitsa iye manjenje, “Ndipo anali ndi vuto mu mnofu,

kuwopa kuti iye angakwezedwe pamwamba pa kuchuluka kwa mavumbulutso.” Mwaona, iye analemba Baibulo, iye anadzozedwa kwambiri. Iye analemba Mabuku a Baibulo. Monga Mose, iye anali mneneri. Kotero iye, Mawu anabwera kwa iye, ndipo iye analemba Ilo, ndipo analoledwa kulowa mu Malemba, Zolemba zopatulika. Tsopano iye anali mmodzi yemwe—yemwe—yemwe akunena akuti . . . amakhulupirira izi, anaphunzitsa zinthu izi.

193 Tsopano kumbukirani kuti Khristu anaukitsidwa kwa akufa ndipo ali pakati pathu. Ndipo muzitengere izo mmalingaliro anu, Khristu anaukitsidwa kwa akufa ndipo ali pakati pathu.

194 Tsopano, ife tawona mitundu yonse ya kusuntha kwakukulu, ndi kufuula ndi kumutamanda Mulungu; zonsezo ndi zabwino. Ife tayankhula mmalirime ndi kunenera, ndi zonse. Ife taziwona izo zonse. Izo nzabwino. Izo zimabwera limodzi ndi Iwo.

195 Koma, kumbukirani, chinthu chotsiriza ndi Kukhalapo Kwake Kwauzimu, Mawu Iwoeni. Iye ndi Mawu. Mutu, Mawu, Iwo akubwera ku Thupi. Mukuona? Ndiyeno Mawu amenewo, mu Ahebri mutu wa 4, anati, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa, ndi amphamvu kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndi ozindikira malingaliro ndi zamkati mwa mtima.” Tsopano mutenge Lemba limenelo ndipo muliyendetse ilo kubwerera mmbuyo kuyambira ku chiyambi cha aneneri, muyendetse izo mpaka mmusi kudutsa mwa Yesu Khristu, ndipo muwone ngati zimenezo si chinthu chomwe chomwecho, chinthu chomwe chomwecho, kuti Iye amadziwika ngati Mesiya.

196 Tsopano si munthu wina pano amene ali Mesiya. Ndi Mzimu Woyera ndiye Mesiya. Khristu ndi Mzimu Woyera ndi chinthu chomwe chomwecho, kotero apa Iwo uli pano tsopano ukungogwira ntchito mthupi, kukonzekeretsa Thupi ku chisomo chokwatulitsa. Mukhulupirire zimenezo, abwenzi.

Ambuye Mulungu, chonde mulole kuti izo zichitike usikuuno.

197 Tsopano mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikutengera mzimu uliwonse muno pansi pa ulamuliro wanga, kwa ulemelero wa Mulungu. Ine ndikunena zimenezo kuti inu mukhoze kumvetsa. Mwaona, sichoncho inu . . .

198 Ngati inu mukukaikira, inu—inu, si chabwino kukhala nthawi yotalika kwambiri, chifukwa anthu ambiri akhala pano, sindikukaikira, awona zimene zimachitika nthawizina kwa osakhulupirira. Izo zimapita kuchokera kwa wina kupita kwa imzake, monga izo zinkachitikira mu Baibulo.

199 Ndi angati a inu pano akupemphera, mukudziwa kuti ndine mlendo, sindikudziwa kanthu za inu? Kwezani mmwamba manja anu, kuti inu mukupemphera, kotero inu mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu.

200 Inu, bambo uyo amene wakhala apo wavala tayi yakuda, mukuyang'ana pa ine pomwe pano.

201 Tsopano taonani. Mukuona Kuwala uko? Kodi inu simukukuwona Iko? Kuwala kwa amba, kobiriwira-mwagolide pansi apa.

202 Kodi inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito Wake, bwana? Ngati Mulungu angakhoze kuwulula kwa ine lomwe liri vuto lanu, kodi inu mukukhulupirira, inu mundikhulupirira ine ndi mtima wanu wonse, inu mukhulupirira kuti anali Mulungu? Kodi inu mungachite izo? Kodi inu mungakhulupirire kuti machiritso anu abwera? Inu muli ndi khadi la pemphero? Ayi, inu mulibe ilo. Inu simukulisowa ilo. Vuto lanu liri mu khutu lanu. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ilo linali mu khutu lanu; izo sichoncho tsopano, ngati inu mukukhulupirira izo. Ine sindikumudziwa bamboyo, sindinayambe ndamuwonapo iye.

203 Tsopano apa pali mwamuna wakhala pafupi ndi inu. Iye akukhala ngati akupemphera. Iye akupempherera chinachake chamuvuta iye. Tandiyang'aneni ine, bwana. Inu muli ndi khadi la pemphero? [M'baleyo akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Inu mulibe. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? ["Inde."] Inu mukukhulupirira zomwe ine ndakuuzani inu, Choonadi? ["Inde, bwana."] Inu mukukhulupirira kuti ndi Kukhalapo kwa Yesu Khristu? ["Inde, bwana."] Inu mukukhulupirira kuti nsana wanu ukhala bwino kuyambira pano? Inu mukutero? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Ngati inu mukhulupirire! Mukuona?

204 Tsopano mfunseni bamboyo. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga. Iye sanandikhudze ine konse. Iye ali mapazi twente kuchokera kwa ine. Kodi iye anakhudza chiyani? Izo zikukwaniritsa Lemba. Iye anakhudza Wansembe Wamkulu. Iye anali atakhala pamenepo, akupemphera kuti achiritsidwe. Onani, iye anakhudza Wamkulu Wansembe amene angakhudzidwe ndi zomverera za zifooko zathu. Mukuona?

205 Tsopano, kodi iwe ukuganiza chiyani, mnyamata wakhala kumbuyo uko, mnyamata akuyang'ana pa ine molunjika chomwecho? Kodi ukukhulupirira kuti Mulungu wachiza vuto la impsyo limene uli nalo? Iwe ukutero? Kweza mmwamba dzanja lako, ngati iwe ukukhulupirira zimenezo. Iwe ukufuna usiye chizolowezi icho chimene uli nacho, aponso, ukazitaye ndudu zimenezo? Gwedeza dzanja lako monga *chonchi* ngati ukutero. Ndiye ukazisiye izo ndipo ukaiwale izo. Yesu Khristu wakuchiza iwe. Ngati ungakhulupirire!

206 Pafupi pomwe ndi inu, pakhala dona atavala magalasi. Iye akuvutika ndi vuto lamanjenje. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu, dona? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati inu mukukhulupirira izo. Chabwino.

207 Kodi inu munganditħandizeko? Pali dona wamng'ono wakhala pafupi ndi inu, akuvutika ndi vuto lachikazi, vuto la dona. Ndiko kulondola, dona. Kwezani mmwamba dzanja lanu, ngati ziri chomwecho. Kuwukha. Ikani dzanja lanu pa iye, kuti iye akhale bwino, chifukwa iye akukhulupirira.

208 Titi, ndiye wakhala pafupi ndi iye, wani, thuu, apo Izo ziri pamwamba pomwe pa dona winayo wakhala pafupi ndi iyeyo. Iye akuvutika ndi miyendo yake, vuto ndi miyendo yake. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza miyendo yanuyo? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndi zimenezotu pamenepo. Mukuona?

209 Inu mukumukhulupirira Iye kuti ali Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse?

210 Inu mukukhulupirira, mwakhala pamenepo? Kuseri komwe kwa bambo uyu wakhala apayu patsogolopa, dona yemwe wakhala *apayu*? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu . . . Inu muli ndi zinthu ziwiri zowopsya. Chimodzi cha izo ndi khansa; chinacho, ndi nyamakazi. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Ngati inu mukutero, kwezani mmwamba dzanja lanu ndi kuti, "Ine—ine ndikukhulupirira." Chabwino, khulupirirani.

Kodi inu mukukhulupirira? Iye akutsimikizira pangano.

211 Apa pali dona wakhala apa akuyang'ana pa ine, kumbuyo komwe kwa bambo uyu. Wavala diresi yofiira yamtundu wina wake. Chofiira, pamwamba *apa*; swetara, iyo ikhoza kukhala. Iye ali patali kwambiri; kuli mdima kunja uko. Zikatha, onani, izo zimakupangitsa iwe kufooka kwambiri, chinthu chonsecho chimangoyamba kukhala ngati mtundu wamkaka kuzungulira mchipinda.

212 Chimene, apo Icho chaima, pamwamba pake pomwe. Mukuona Kuwala uko? Iye akupempherera chinachake. Ngati Yesu Khristu ati awulule kwa ine zomwe inu mukuzipempherera, kodi inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Inu mutero? Ndine mlendo kwa inu, ndipo ndinu mlendo kwa ine. Koma inu munakhudzana ndi Wansembe Wamkulu, chifukwa chizindikiro chimene Iye amandipatsa ine chiri pa inuyo pomwe, mwaona, mwaona, chizindikiro. Ine ndikudziwa icho chiri.

213 Inu muli ndi vuto lalikulu lamanjenje limene inu mukuvutika nalo. Ndiponso inu muli ndi chotupa pakhosi, chimene mukuvutika nacho. Ngati uko nkulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu.

Inu mukuti, "Inu mukhoza kuziwona zimenezo."

214 Chabwino, inu bwerani . . . Sindinu wochokera kuno. Inu bwerani . . . Sindinu wochokera ku dziko lino, malo ano. Inu mukuchokera ku Memphis. Uko nkulondola.

215 Dona amene wakhala pafupi ndi inu, iye nayenso akuchokera ku Memphis. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, dona? Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchizani inu? Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, kapena wantchito Wake? Izo zimawapunthwitsa anthu, mwaona. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Inu mukukhulupirira kuti ndi Mulungu amene akuchita kuyankhula uku? Inu mukudziwa kuti ine sindingadziwe kanthu za inu. Inu mukukhulupirira kuti angakhala ali Mulungu ndiye? Chabwino. Inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Ndipo muli, chimene inu mukuvutika nacho, inu muli ndi . . . inu muli ndi vuto ndi kummero kwanu, nanunso. Ndipo chinthu china, inu muli ndi mfundo, chotupa kumbali kwanu. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine mbali imene icho chiri? Ngati ndi choncho, kwezani mmwamba dzanja lanu ngati ine ndikukuuzani inu choonadi. Icho chiri kumbali ya kumanja. Mukuona? Mukuona? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? Kodi izo zikuthandizani inu? Ndinu Akazi a Cox. Uko nkulondola. Mukuona? Bwererani, mwaona.

216 Kodi inu mukukhulupirira? Nonse a inu mukukhulupirira tsopano? Mwaona, ndiko kutsimikizira kwa pangano kwa Mbewu ya Abrahamu, ngati inu mungakhulupirire! Mukuona?

217 Pano, pali mkazi wamng'ono wagona apa pa machira. Kodi inu mukukhoza kundimva ine, dona, mwagona pa machira amenewo? Eya. Ine sindingakhoze kukuchizani inu. Ine sindikudziwa kanthu za inu; ndinu mlendo basi kwa ine. Koma kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu Khristu akhoza kuwulula kwa ine lomwe liri vuto lanu? Kodi zimenezo zingakuthandizeni inu? Zikhoza, izo zingatero? Ngati mugone pamenepo, inu mufa. Inu muli nawo mwayi umodzi wokha wokhala moyo, ndiwo kumulandira Khristu. Inu muli ndi khansa. Uko ndi kulondola. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu tsopano? Inu mukutero? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati inu mukukhulupirira zimenezo. Chabwino. Pamene mulipo, chinthu chokha chimene inu mungakhoze kuchita, chingakhale kudzuka kuchoka pa bedi limenelo; ndi kutenga chimene inu mwagonapocho, ndi kumapita kwanu, kumadzinenera chikhulupiriro chanu mwa Mulungu, monga Mbewu ya Abrahamu. Dzukani, mu Dzina la Yesu.

Mwaona, iye akudzuka, kuti atenge lonjezo lake mwa Mulungu.

218 Ndi angati nonse a inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse tsopano?

219 Imiririrani. Inu muli ndi mphamvu; Mulungu akupatsani inu mphamvu. Imiririrani, pa mapazi anu. Ndi uyo apo, wadzuka, kuchoka pa machira.

220 Tsopano nonse a inu mukufuna kuti mumulandire Yesu Khristu, imirirani pa mapazi anu. Imirirani pa mapazi anu. Imirirani, paliponse, mulandireni Yesu Khristu ngati mchiritsi wanu.

221 Ambuye Yesu, chiritsani mmodzi aliyense wa iwo. Perekani izi, Ambuye.

64-0402 Yehova-Yire #1
4-H Club Barn
Louisville, Mississippi U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org